


UBATIZO WA MZIMU WOYERA

 Ndithudi ndakondwa kwambiri kuwona ochuluka chotere atatuluka usikuuno, ine nditakusungani inu kale mpaka pakati pausiku usiku wathawu. Ine sindimaganiza kuti nonse mukadatuluka lero, koma zikuwoneka ngati mukuti mubwere ku Sande sukulu, ndipo ndi zabwino kwambiri.

² Tsopano ife tikuphunzira ndi kuyesera kungotenga nthawi yathu pa Chiphunzitso cha mpingo ichi. Ndipo ine ndimangophunzitsa Icho. Tsopano pakhoza kukhala pali alendo ena ali ndi ife, omwe ine sindikuwadziwa. Ine sindimakhala muno mu kachisi mokwanira kuti ndizidziwa omwe ali mamembala a mpingo. Koma ine ndinalengeza kuti uno udzangokhala wa mamembala a mpingo. Chifukwa, kunja, anthu ali ndi ziphunzitso zambiri zosiyana, ndi zina zotero. Chabwino, ndipo, iwo amakhulupirira zinthu zimenezo. Iwo anaphunzitsidwa kuti azizikhulupirira izo. Ndi—ndi—ndiyeno pamene iwe ubwera mu mpingo wina, mwinamwake, ndipo nkuphunzitsa chinachake chosiyana kwambiri, chabwino, ndiye iwo amaganiza, “Ndikuti, ine sindikugwirizana nazo Izo.” Mwaona? Chabwino, ife sitikutanthauza kuti tikhale amwano kapena kuti timpweteke wina aliyense, chifukwa chimene ife tikuchitira izi. Tsopano, inu muzikhulupirira chirichonse chimene inu mukukhumba. Koma ife tiri . . . ine ndikuyika izi, ndipo ndiyenera kuzipanga izo mwamphamvu kwenikweni, chifukwa ife tiyenera kuti tizikhomerere izo pansu. Izi ndi zomwe kachisiyu amayima nazo, mwaona, basi zomwe ife timaima nazo pano. Ndipo, mwanjira imeneyo, ife sitingafune kuti inu zikukwiyitseni ndi kumaganiza kuti ife timayesera kuti tikupwetekeni inu mu chikhulupiriro chanu, kapena chirichonse chonga izo. Sindizo nkomwe. Ndipo izi ndi . . .

³ Ife timadutsa mu izi pafupi zaka ziwiri kapena zitatu, kunoko, ndi chomwe ife timaima nacho, chiphunzitso basi, chimene ife timaima nacho, ndi chifukwa chomwe ife timachitira izo. Chomwe, chifukwa chake ife timakhulupirira Izi. Ndipo kotero ngati pangakhale alendo muno omwe sali m—membala wa mpingo, ndife ndithudi okondwa kukhala nanu mutakhala pa zokambirana izi mmawa uno ndiponso usikuuno.

⁴ Ndipo, ndiye, Lachitatu padzayambika msonkhano wokopa wachizolowezi mu msonkhano, ine ndikutanthauza, ku kachisi kuno. Ndipo ine ndakhala nditachokapo kwa kanthawi, kukapuma pang’ono. Ine ndinatopa zedi, kwenikweni, ndipo ndimayenera kuti ndichokepo, kuti ndikapume kwa kanthawi. Ndipo ine ndangobwera kumene, ndikumverera bwino, ndikumverera modabwitsa. Ndipo kotero ine ndikhala ndikuchokanso, mwamsanga izi zikatha, ndipo

ine sindibwereranso mpaka Januwale. Ine sindikupita ku misonkhano iliyonse; ine ndikungochokapo, kukapitiriza kupuma komwe ine ndinalimoku.

⁵ Koma, pamene ife tinabwera muno, ife tinadzaupeza mpingo utakhala ngati uli mu kusokonezeka pang'ono apa ndi apo, ndi ena a mamembala atayamba kukhala ngati akumafunda pang'ono, kumachokapo, kumasungirana maudani pang'ono kwa wina ndi mzake, ndi zina zotero monga choncho. Ine ndinazungulira, kuchokera kwa mmodzi mpaka kwa wina, mpaka ife tazikonza zonse izi mowongoka tsopano. Ziri bwino. Mwaona?

⁶ Ndipo palibe cholakwika chirichonse. Panalibe cholakwika chirichonse ndi aliyense wa mamembala. Aliyense wa iwo ndi amuna ndi akazi abwino. Ngati iwo atangozindikira kuti uyo ndi Mdierekezi, akufika pakati pa anthu. Ndizo ndendende kulondola. Si anthuwo. Ngati inu mungakhoze kumulola m'bale kuti awone izo, ndiye iye sangakhoze kusunga udani ndi munthu winayo. Iye ali. . . I—iye amverera kuipa. Iye amverera monga, “Chabwino, izo. . . ine ndikumumvera chisoni m'bale wanga.” Mwaona, ngati iye anachita molakwitsa, bwanji, sanali m'baleyo. Anali Mdierekezi yemwe anachita izo.

⁷ Inu mukati, “Chabwino, munthu uyu anachita chinthu *chakuti, chakuti.*” M'bale wanu sanachite izo; mlongo wanu sanachite izo; ameneyo anali Mdierekezi analowa mwa iwo, amene anachita izo. Kotero musati mumutsutse m'baleyo, mlongo; muzimutsutsa Mdierekezi, ndi yemwe anayambitsa izo.

⁸ Ndipo kotero tsopano mu Ziphunzitso za mpingo izi, tsopano, izo zikhoza kukhala zosamvetseka kwambiri kwa inu. Izo zikhoza kukhala kuti inu simungagwirizane nazo, nkomwe. Koma ife basi. . . Ndi zomwe ife timakhulupirira. Ife timakhulupirira izo chifukwa izo ziri mu Baibulo, ndipo ife timaphunzitsa izo mwanjira imeneyo.

⁹ Tsopano, usiku watha, phunziro lathu linali: *Nchifukwa Chiani Ife Sitiri Chipembedzo?* Tsopano, ife ndife bungwe chifukwa ndife mpingo, koma ife sitiri chipembedzo. Ndiyeno ine ndimapereka zifukwa zomwe ife sitiri chipembedzo.

¹⁰ Tsopano, pamene ife tikutsegula zokambiranazi mmawa uno, ife tisanachite chomwecho, tiyeni ife tipemphere.

¹¹ Wokonedwa Mulungu, ndi mu Kukhalapo Kwanu Koyera momwe ife tikudza kachiwiri kudzapempha kuyeretsa kwa malingaliro athu omwe, solo zathu, kuti tikhoze kudzipereka tokha kwa Inu ngati chida momwe Inu mungakhoze kumagwiriramo ntchito, ndi kupyoleramo, kwa ulemerero Wanu womwe. Ndipo, Atate, yeretsani maganizo anga, ndi malingaliro anga, ndi kuyankhula kwanga, kuti zisati zikhale ine yemwe ndizichita kuyankhulako; koma Mzimu Woyera uzidzoza milomo, ndipo ya donga, kuti ikhoze kumabweretsa Zoonadi

zomwe Mulungu Wamphamvuzonse angafune kuti Mpingo Wake uzidziwe.

¹² Ndipo ife tati tikupempheni Inu, ndiye, Ambuye, ngati Inu muchita izo, kuti Inu muchikankhire mmbuyo chiwanda chirichonse cha—cha vuto, ndi chiwanda chirichonse cha udani ndi matetano, zichoke kwa anthu, kuti iwo akhoze kumamvera Mzimu Woyera ukuyankhula, kuti Mulungu akhoze kulandira ulemmero kuchokera mu kusunkhana kwathu limodzi mmawa uno. Ndipo ngati pati pakhale chinthu chimodzi mu mitima yathu chimene sichiri ndendende basi mu chikhalidwe, pamene Inu mungakhoze kuyankhula kwa ife, O Mulungu, chiponyerani icho kutali ndi ife, utali wa momwe Kumawa kuliri kwa Kumadzulo. Pakuti, ife tikufuna tizidziwa chifuniro cha Mulungu chokha, kuti tizichichita. Chotero titsogolerani ife mwa Mzimu Wanu Woyera, mu zokambirana zomwe zikudzazi pa Mpingo ndi Chiphunzitso Chake, ndi Chomwe Iwo uyenera kumaima nacho, ndi chifukwa chimene Iwo uyenera kumaimira izo. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

¹³ Tsopano, usiku watha ife tinali kupereka l—lingaliro la chifukwa chimene ife sitinali chipembedzo chopangidwa bungwe. Ndipo ife... Maziko pang'ono okha kwa izi. Ndi chifukwa ife tikupeza, kuti, mu chipembedzo, izo zimalemba zotchinga.

¹⁴ Tsopano, ife tiri nazo zinthu zambiri zoti tikambirane. Ndipo ife tinakambirana izo, chifukwa chimene ife sitimalola azitumiki achikazi mu mpingo, usiku watha.

Ndipo mmawa uno ife tikufuna kuti, phunziro, ngati nkotheke: *Ubatizo Wa Mzimu Woyera*, ndi chifukwa chimene ife timakhulupirira mu ubatizo wa Mzimu Woyera, ndi momwe ubatizo wa Mzimu Woyera umabwerera, ndi chomwe Iwo umachita, ndi momwe Iwo umakupangitsira iwe kumachita pambuyo pake.

¹⁵ Ndiyeno usikuuno, ngati Ambuye alola, ine ndikufuna ndiyankhule pa phunziro la, “Mbewu ya serpenti, ya iye mu tsiku lino.” Tsopano, anthu samakhulupirira mu mbewu ya serpenti, koma ndi Lemba. Mwaona? Tsopano, mosasamala za . . .

¹⁶ Tsopano, ichi, ngati ine ndingachipange ichi molimba kwenikweni, ine sindikutanthauza izo tsopano kwa inu—kwa inu anthu okonedwa. Chinthu chokha chimene ine ndikuyesera kuti ndichite ndi kuchilondolera icho mkati, ndipo ife tichipanga icho mowawa, onani. Kotero iwe uyenera kuyankhula monga . . . Iwe ukati, “Johnny, pita ukakhale pansu,” iye mwina sangati amvetsere kwa izo. Koma iwe ukati, “Johnny, khala pansu!” Johnny apereka chidwi chochuluka kwa izo. Kotero tsopano ife tikuti tifuule, “Johnny, khala pansu,” mmawa uno. Chabwino. Ine ndikufuna kuti ndiyankhule izo mwakuti inu mumvetse chimene ife tikutanthauza. Mwaona?

17 Ndipo ngati ife titi tinene chinachake chomwe chiri chosiyana ndi malingaliro anu, ndi chikhulupiriro chanu, sindife chinthu chimodzi. . . Kumbukirani, kuti, mu mpingo uno pokhala azipembedzozosiyana, ife timakhulupirira kuti wa Chibaptisti, Chimethodisti, Chipresbateria, Chilutera, Chikatolika, Chiprotestanti, Myuda, yense yemwe ali, bola ngati iye ali m'bale, iye ndi m'bale wathu, ndizo zonse, ziribe kanthu chipembedzo chimene iye alimo. Mulungu sadzamutsutsa nacho konse iye, pokhala mu chipembedzo.

18 Koma, chifukwa chomwe zipembedzo ziri. Tsopano, izi ndi zomwe zimayambitsa zipembedzo. Mulungu amaulula chinachake chaching'ono kwa winawake, ndipo iwo amabwera ndi kudzapanga chipembedzo mozungulira kachikhulupiriro kameneko komwe iwo ali nako, ndiyeno Mulungu sangakhoze kusunthira patsogolo paliponse.

19 Amethodisti angakhoze bwanji kulandira chirichonse kuposa ntchito yachiwiri ya chisomo? Iwo anadzipanga okha chipembedzo pansi pa izo. Abaptisti angakhoze bwanji kukhulupirira konse chirichonse kuposa chimene iwo. . . "Olungama. . ." Kapena, Achilutera, kani, "Olungama azikhala moyo mwa chikhulupiriro." Ndi chomwe iwo anadzachitirapo chipembedzo. Akanakhoza bwanji Abaptisti kupita patsogolo paliponse kuposa momwe iwo amapitira? "Chifukwa, pamene iwe ukhulupirira, iwe umalandira Mzimu Woyera. Ndi kumizidwa mmadzi, ndipo icho chimakhazikitsa izo." Chifukwa? Ndi chimene iwo anachitirapo chipembedzo. Mwaona? Nchifukwa chiani kuti Apentekoste amakhulupirira, kuti, "Pamene iwe uyankhula mmalirime, iwe uli nao Mzimu Woyera, ndipo izo zimakhazikitsa izo?" Chifukwa iwo apangira chipembedzo pansi pa icho. M'bale, zinthu zimenezo zikhoza kukhalapo, chimodzi chirichonse, chabwino bwino, koma Mulungu samamangidwira ku kachipembedzo kakang'ono kalikonse. Iye amangoziyala pa chinthu chonsecho, ndizo zonse. Ndi—ndipo ife—ife timakhulupirira izo.

20 Ndipo ndi chifukwa kuti ife sitinakhale konse chipembedzo. Ambuye atipatsa ife mwayi wougwirizanitsa mpingo waung'ono uno mu zipembedzo zambiri zosiyana, koma ife sitimachita izo. Chifukwa, ife tikufuna kuti tizikhala monga chonchi basi chotero iwo ukhoze kukhala pansi pa ulamuliro ndi umutu wa Yesu Khristu. Ndiko kulondola. Chirichonse chimene Iye awululira kwa ife, ndipo ife nkuwona kuti ndi Choonadi, ndipo icho chikufola ndi Mawu Ake, njira yonse mmbuyo ndi mtsogolo kudutsa mu Baibulo, kuti icho ndi Choonadi, ndipo Mzimu ukumavomerezero pa izo, ife tiribe zotchinga za chipembedzo zoti zitiletse ife kuti tivomereze Icho. Ife timapita patsogolo pomwe kulowa mu Icho, ndi kumasunthira patsogolo pomwe.

21 Ndipo kotero pamene chipembedzo chinena izo, monga mpingo wa Khristu, iwo ali pansi pa chipembedzo, otchedwa

mpingo wa Khristu, kuti, “Masiku a zozizwitsa anatha, ndi zinthu zonse izi monga choncho.” Nanga, inu mungazipeze konse kuti izo mu Lemba? Koma iwo sakanakhoza kuchita kanthu kalikonse nazo. Iwo apanga chipembedzo pansu pa izo, mwaona, kotero palibe kanthu komwe inu mungakhoze kuchita nazo.

Koma ife tikufuna kuti tikhale afulu, pamene ife tingakhoze kumayenda monga Mzimu ukutisunthira ife, mwa kuya kozama ndi pamwamba pokwera, ndi kumangomasunthabe mopitirira, ndi kupitirira, ndi kupitirira, ndi kupitirira, ndi kupitirira, ndi kupitirira, basi kulikonseko.

²² Koma tsopano ife sitivomereza zotengeka zirizonse. Ife tilemba mzere apo pomwe. Ngati winawake apeza kenakake kakang’ono kamene Ambuye awululira kwa iye, ndipo izo sizikugwirizana ndi Baibulo ili, mpaka kudutsa mu Baibuloli kuyambira Genesis mpaka Chivumbulutso, nkukhala kachiphunzitso, ndiye ife sitizivomereza izo. Mwaona? Izo ziyenera kumabwera kuchokera mu Baibulo. Ndipo izo sizingangobwera ndi vumbulutso la winawake. Ngati vumbulutso likugwirizana ndi Mawu, chabwino.

²³ Bambo anabwera kwa ine, nthawi ina kale, ndipo iye nati, “Ine ndangobwera kuchokera ku United States, M’bale Branham.” Iye anati, “Tsopano, ine ndadziwana ndi mlongo wa Chikhristu, ndipo,” anati, “mlongo wa Chikhristu uyu anali mmodzi wa akazi okondeka kwambiri. Koma,” anati, “iwo anafika popeza kuti iye anali ndi amuna atatu kapena anayi. Ndipo,” anati, “ku—kuti, pamene ine ndamudziwa iye, chikhalireni kuno miyezi itatu, iye anamuchotsa winayo ndi kukwatirana ndi wina.” Ndipo anati, “Iye anali nawo Mzimu Woyera, amayankhula mu malirime kwathunthu nthawizonse, mwachizolowezi, ndipo,” anati, “amapereka maulosi ndi vumbulutso.” Anati, “Iye ndi mkazi wodzazidwa Mzimu kwenikweni. Ndipo iye anali mtumiki wamkazi.” Ndipo anati, “Ine ndinapita ndipo ine ndinakawafunsa Ambuye, ‘Bwanji chinthu *chakuti-n-chakuti* chiri? Bwanji kuti mkazi uyu angamachite zonga izi?’” Ndipo anati, “Ine ndinali ndi loto la mkazi wanga. Ndipo mkazi wanga anali akumagona ndi mwamuna wina, chimene chinali makhalidwe oyipa. Ndiyeno,” anati, “iye anadza ndipo anadzagwada pansu pafupi ndi mapazi anga nati, ‘Kodi inu mungandikhululukire ine pa zomwe ndazichita?’” Iye anati, “‘Zedi, ine ndakukhululukira iwe.’ Ndipo anati, ‘Nchifukwa chiani iwe ukundikhululukira ine mosavuta?’ Anati, ‘Chifukwa ine ndimakukonda iwe.’” Ndipo anati, “Ambuye anandiyankhulanso mu loto ndipo anandiuza ine, izo. ‘Ndi chifukwa ine ndinamukhululukira iye, chifukwa ine ndimamukonda iye.’”

²⁴ Ine ndinati, “Bwana, loto lanu linali lokoma mwamphamvu. Ilo linali labwino mwamphamvu, koma Ambuye sanakupatseni konse inu loto limenelo. Ilo silikugwirizana ndi Mawu

Ake.” Ndiko kulondola. Ilo siligwira ntchito ndi Mawu Ake. Ziribe kanthu kuti ilo likuwoneka lenileni chotani, ziyenera kumachokera mu Mawu.

²⁵ Mu Chipangano Chakale, iwo anali nazo njira zitatatu zodziwira uthenga. Yoyamba, ndithudi, inali lamulo; yotsatira, inali ndi mneneri; yotsatira, ndiyo ndi wolota. Tsopano, lamulo linali zinthu zolembedwa zomwe zinkasungidwa mu likasa, ndipo izo zinali malangizo ndi malamulo pa malangizo. Ndiyeno mneneri ankakhoza kunenera, kapena wolota ankakhoza kulota loto. Chimene, Mulungu amachita nazo njira zonsezo, ndi aneneri ndiponso ndi maloto. “Ngati pakhala pali wina pakati panu yemwe ali wauzimu, kapena mneneri, Ine Ambuye ndizidziwitsa Ndekha kwa iye mu—mu—maloto, ndipo ndizidziulula Ndekha kwa iye mu masomphenya. Ndipo ngati zomwe iye anena zifika pochitika, ndiye muzimumvera iye, pakuti Ine ndiri ndi iye. Ngati izo sizitero, ndiye musamamumvere iye.”

²⁶ Tsopano, pamene iwo amutenga mlosi, mneneri, kapena wolota, ndipo (iwo) iye atakhala nalo loto kapena ulosi, ndipo iwo amafuna kuti apeze ngati izo zinali zoonza kapena ayi, iwo ankamutengera iye uko ku chimene chinkatchedwa Urimu Tumimu.

²⁷ Tsopano, ine ndikudziwa izo zikhoza kukhala, kwa ena—ena a inu, mawu ovuta pang’ono. Koma zomwe izo zinali, zinali makamaka... Aroni pokhala wansembe wamkulu pa—mafuko khumi ndi awiri a Israeli, iye anali ndi miyala sikisi pa mbali iliyonse ya chapachifuwa. Ndipo mwala uliwonse unali mwala wakubadwa wa fuko, monga fuko la Yuda, fuko la Gadi, fuko la Rubeni, fuko la Benjamini. Lirilonse linali ndi mwala wakubadwa. Ndiyeno pamene mwala wakubadwa uja... Icho chimakhala chitapachikidwa pa imodzi ya mbale mu mpingo, kapena pulasitala. Ndiyeno pamene iwo ankamubweretsa mneneri uyu yemwe anali ndi uneneri umene iye ankati Ambuye achita chinthu chinachake, ndipo iwo ankamubweretsa iye patsogolo apa, ndipo iye ankanena uneneri wake, kapena iye ankanena loto lakelo. Tsopano, ngati Mulungu anali mu loto limenelo kapena mu ulosi umenewo, nyali zimenezo zinkayamba kusakanizikana limodzi ndi kumapangika ngati mtundu wa utawaleza ukunyezimira, yankho la Chauzimu. Mwaona? Ndiko kulondola. Kuvomerezana ndi mwala uliwonse mmenemo, mwala uliwonse kumasakanizitsa gawo lake palimodzi, kunyezimiritsanso mwa yankho la Mulungu, “Munthu uyo ndi mneneri. Iye akunena zoonza.” Kapena, “Loto limenelo linatumizidwa ndi Ine.” Koma ngati izo zinangokhala matalala ndipo sizinasunthe, ine sindikusamala momwe izo zimawonekera ngati zenizeni, izo zinali zolakwika. Iwo sanali kuzilandira izo.

²⁸ Ndi kufotokoza kokongola bwanji lero. Tsopano, Urimu Tumimu wa Chipangano Chakale anathetsedwapo, chifukwa anasintha unsembe. Tsopano Urimu Tumimu ndi Mawu a Mulungu, Baibulo. Inde, bwana. Mkati umu, Baibulo linati, “Mulole mawu a munthu aliyense akhale bodza, ndipo Anga akhale owona.” Ndipo ziribe kanthu momwe zikuwonekera ngati zenizeni pamene munthu akuzinena izo, kapena momwe loto lake liriri lenileni, kapena vumbulutso lake liri, ngati izo, Bukhu lirilonse mu Baibulo, Baibulo lonse, silikunyezimiritsa kuwala pa Ilo, kuti ndi Choonadi, zisiyeni izo zokha, zisiyeni izo zokha.

²⁹ Tsopano, inu mukhoza kutenga chidutswa chaching’ono cha Lemba pano, nkuti, “Yesu anachita *zakuti-n-zakuti* ndipo ife tiyenera kumachita zomwezo,” inu mukhoza kuwapanga Iwo kunena chirichonse chimene inu mukufuna kuti Iwo anene. Koma izo ziyenera kumabwera njira yonse modutsa ndi kufola mwangwiwo ndi Mawu a Mulungu, ndiye ndi zolondola, uyo ndi Mulungu akunena chomwecho. *Uyu* ndiye Urimu ndi Tumimu Wake.

³⁰ Chotero, Mulungu sanayambe, mu m’badwo uliwonse, wakhalapo ndi mipingo yachipembedzo. Inu mundiuze ine pamene izo zinali. Ndipo, tsopano, panalibe konse chipembedzo mpaka zaka firii handiredi ndi sikisite pambuyo pa imfa ya mtumwi wotsiriza. Uwo unali mpingo wa Roma Katolika. Ndipo kuchokera mu... Mpingo wa Roma Katolika, Mulungu anawutcha iwo, mu Baibulo, Chivumbulutso 17, “hule.” Uyo ndi mkazi wosayera. Ndipo kuchokera umo, iye anali nawo ana aakazi, ndipo ana aakazi amenewo achiwerewere, osayera monga iye analiri. Ndi chimene Lemba limanena. Ndipo mpingo wa Roma Katolika unabala chiprotestanti chonse, ndipo iwo anapita mmbuyo momwe ndipo anachita chinthu chomwecho chimene iye anachichita.

³¹ Ndipo chifukwa chimene iye analiri wosayera, iye anali ndi chikho cha ziphunzitso mu dzanja lake, vinyo wa mkwiyo wake wa zaziwerewere zake. Ndipo iye ankachipereka icho kwa mafumu a padziko lapansi, ndipo iye anakhala “pa madzi ambiri,” ndipo ankalamulira pa olamulira a padziko lapansi. Ife tinazipeza izo chomwecho mu Baibulo. Ife tinapeza kuti iye akuyenera kuti azikhala pa mapiri seveni, mpingowo. Ife tinazipeza izo. Ife tinapeza kuti iye anakometseredwa ndi nduwira yapatatu: ulamuliro wa gehena, kumwamba, ndi purigatorio. Kulondola. Ndipo ndi mwamuna yemwe anali wolamulira mmenemo; iye anali wotsutsakhristu, atakhala mu kachisi wa Mulungu, akudzisonyeza yekha kuti iye anali Mulungu, akukhulukukira machimo pa dziko lapansi. Ife tinali nazo zonse izi, tinadutsa mu izo ndipo tinawona kuti izo ndi zokhoza.

³² Akuti, “Pano ziri, kwa iye yemwe ali nayo nzeru.” Ife tikupeza kuti Mzimuwo unapitirira kuyankhula

mwachimvekere, “Kwa iye yemwe ali nayo nzeru; kwa iye yemwe ali nacho chidziwitso; kwa iye, mizimu yosiyana, mphatso.” Kodi inu simungakhoze kuwona kuti Mulungu akuwuyendetsa Mpingo umenewo mu masiku otsirizawa? Payenera kuti pawuke Mpingo wodzaza ndi mphatso zauzimu, mphatso zenizeni za Mulungu. “Pano ziri kwa iye yemwe ali nayo nzeru. Muloleni iye awerenge chiwerengero cha chirombocho, pakuti ndi chiwerengero cha munthu. Chiwerengero chake ndi sikisi handiredi ndi sikisite-sikisi.” Ndipo ife tinapeza pamene izo zinali, ndendende. Sizikanakhoza kukhala moonjezeranso zangwiwo. Lembani izo, enianu, “vicarivs,” chomwe chiri wolowa mmalo mwa Khristu, “filii” wa Mulungu, *VICARIVS FILII DEI*, ndipo muwone ngati siziri, mu kuwerengera kwa Chiroma, ndipo muwone ngati simupeza sikisi handiredi ndi sikisite-sikisi. Muwone ngati si mukuika, osati pa china chirichonse zomwe zikanakupatsani inu kukaikira pa *izi* kapena *izo*, koma pa malo omwewo pamene Malemba ena onse amati iwo ukanati udzakhale uli.

³³ Ndipo ndi ife pano, Achiprotestanti, tikutulukira poyera pomwe. Tsopano, chimene ife tikuyesera kuti tichite lero ndi kubweretsa izo ndi kusonyeza kuti chiphunzitso chimene mpingo wa Katolika unachibweretsa, ndipo uli nacho, ife tachitenga icho komwe kuno mu mpingo wa Chiprotestanti. Ndipo ife tikuchipereka icho kwa anthu, chomwe chiri chikho chomwecho cha ziwerewere zauzimu chimene iye akuzipereka. Chifukwa, izo siziri Mwamalemba. Izo ndi ndi zopangidwa ndi anthu. Iwo ndi uneneri wabodza. Uwo ndi bodza. Izo ndi za Mdierekezi.

³⁴ Ndiyeno ife tinapeza, kuti tipeze maziko pang’ono, kuti tisonyeze izo, m’badwo umene ife tiri kukhalamo. Ndipo tinazitenga izo usiku wathawu, kuti, m—mwana wobadwa pathengo, mwana wachigololo, sankakhoza ngakhale kulowa mu msonkhano wa Ambuye kwa timibadwo fortini. Izo zingakhale zaka foro handiredi; zaka forte kwa kam’badwo. Momwe tchimo linaliri loyipa! Ndi momwe liriri loyipa, osati linali, koma chomwe ilo liri tsopano. Ndipo ngati izo zinali pansu pa lamulo. . .

³⁵ Ndipo Khristu anabwera kudzalikulitsa lamulo. Iye anati, “Inu munawamva iwo akuti, iwo a nthawi zakale, ‘Musati muzipha ayi’; koma Ine ndikuti kwa inu, yense yemwe amukwiwira m’bale wake, popanda chifukwa, wapha kale.” Analikulitsa ilo. “Inu munawamva iwo akuti, iwo a nthawi zakale, ‘Inu musati muzichita chigololo,’ ako kanali kachitidwe; koma Ine ndikunena kwa inu, yense yemwe ayang’ana pa mkazi, ndi kumukhumbira iye, wachita chigololo.” Analikulitsa ilo, kanthawi zikwi. Chabwino, ngati izo zinkatengera timibadwo fortini kuti ilo lizimirire, ndiye nanga bwanji pamene galasi lokulitsira la Mulungu laponyedwera pa ilo?

³⁶ Ndipo anthu lero, ausinkhu wa mmateni uko mma high school, akumakhala ndi maphwando a mowa, ndi kumamwa, ndi kumakhala...ndi asungwana aang'ono, kumakhala mu chigololo, anyamata aang'ono, ndi zinthu zonga izo. Ndi kam'badwo ka mtundu wanji kamene kakubwera ukatha uno? Nchiani chikuwapangitsa asungwana aang'ono awa kumachita monga choncho? Mayi wawo anali wodzivula, agogo awo aakazi anali msungwana wa makolasi. Ndipo Iye anati Iye adzachezera kusaweruzika kwa makolo pa ana ndi ana a ana, mpaka ku kam'badwo kachitatu ndi kachinai. Inu mungakhoze kuyembekezera chiani chinanso?

³⁷ Ndipo pamene zinthu zonsezo ziyamba kuwukha, ndipo mbewu yolungama nkuyamba kukhala cha pambali, kuyamba kuwondela wondela. Ndipo oyipa nkumangopitirirabe, achipembedzo kwambiri, kumangoipira ipirabe, ndi kuyipira ipirabe, palibe china choti nkuchita koma kuchiwononga chinthu chonsecho monga Iye anachitira kumbuyo uko mu kuwononga kwa chigumula. Lingaliro lirilonse la munthu liri kupitirira kudzaza ndi tchimo. Chirichonse chimene munthu amachiganizira lero ndi botolo la kachasu, kapena mkazi wina, kapena kukathamanga thamanga uko, osakhoza kukhala moyo wona kwa akazi awo. Anyamata osakhoza kukhala mowona kwa asungwana awo. Asungwana osakhoza kukhala moonna kwa anyamata. Chifukwa, iwo ali pa malo otero mpaka Mdierekezi wawamanga iwo ndi kuwagwira ndi mizimu yoipa, chinthu chonse chakhala chisakaniziko cha tchimo. Ndi chifukwa ife tiri mu tsikuli. Ndipo nchifukwa kuti Russia akusewera ndendende mmanja a Mulungu, kuti achichotsepo chinthu ichi kuno. Baibulo limanena chomwecho. Ndithudi. Mulungu akugwiritsa ntchito chikominisi. Iye adzachigwiritsa ntchito icho. Chikominisi chidzawononga chinthu chonsechi, molingana ndi Lemba, ndipo ife tiri mu tsiku limenelo.

³⁸ Tsopano, pobweretsa zinthu izi poyera, onani. Mveterani, anthu, inu mukuyang'anizana nazo izi. Ndipo inu, izo... Izo zikutsimikizira kopita kwanu Kwamuyaya, koteru musati muzitenge ngati chinachake mopepuka. Muziyang'ane izo mu—Urimu Tumimu yemwe akupangitsa, momwe zikuwapangitsira Mawu.

³⁹ Tsopano, pamene ife tikuyankhula za zinthu izi, muwone ngati izo zikugwirizana nalo Baibulo, muwone ngati izo zikumangirizana nazo zomwe Lemba linanena.

⁴⁰ Tsopano, mpingo uliwonse, pamene inu mukuti, “Ndine Mkhristu.” “Ndinu wa chipembedzo chiti?” Kodi izo zimapanga kusiyana kwanji, chipembedzo chomwe iwe ulimo? Ife tikuzindikira kuti chipembedzo chiribe kanthu kochita nalo Baibulo la Mulungu. Ndipo zipembedzo zonse za Chiprotestanti ndi timahule. Baibulo lanu limanena chomwecho. Pamene inu munena kuti ndinu wa Methodisti, ndinu kahule ka

Chimethodisti. Inu mukati ndinu wa Baptisti, ndinu kahule ka Chibaptisti. Pamene inu mukuti ndinu wa Pentekoste, ndinu kahule ka Chipentekoste. Ndi zomwe Baibulo linanena. Kotero, iye ali, “Mayi wa timahule.” Tsopano, ngati ndi zonse zomwe inu muli nazo. . .

⁴¹ Tsopano, ngati inu mumayanjana nao mu chipembedzo ichi komabe muli Mkhristu, ndinu Mkhristu; ndipo sindinu wa Methodisti, sindinu wa Baptisti, sindinu wa Chipentekoste. Ndinu Mkhristu. Osati, poti, ngakhale. . .

⁴² Ine ndinamva zokambirana mmawa uno pa wailesi, pamene ine ndimakonzekera kuti ndibwere ku tchalitchi, pa kukambirana kwa Chikhristu atazungulira tebulo uko mu Louisville. Ndipo mipingo yatengera dongosolo la kuphunzitsa ana awo kamwedwe kamakono.

Ndi mtundu wanji wa zizete ife titi tipange? Chifukwa chiani ziri choncho? Chifukwa amayi awo ndi abambo kunyumba samadziwa konse za Mulungu kuposa momwe Akafula amadziwira za walupanga waku Igupto. Chokani ku chinthu chonsecho. Inu simukusowa makono. . . kudzipanga nokha amakono. Inu mupanga zidakhwa pamene inu muzichita izo. “O, ife tizimulola iye kumachita *izi*, ndi kumulola iye kumachita *izi*,” ndi zina zotero monga choncho. Inu mungayembekezere chianinso? Ife sitingakhoze kupita kam’badwo kena. Ife sitingakhoze kuchita izo. Ife tiri pa nthawi yotsiriza.

⁴³ Chotero, ine sindikufuna kuti inu mundiyike ine mu gulu lina la chidempete. Ine ndikhoza kukhala ndiri; ngati ine ndiri, ine ndiri basi monga. . . Ndine wosadziwa izo.

⁴⁴ Ine ndinanena kwa mkazi wanga wakhala apoyo. Ine ndinati, “Meda, kodi ine ndakhala wotentheka wachipembedzo? Kodi ine ndasokonezeka malingaliro anga? Kapena, kodi ndi Mzimu wa Mulungu umene sungakhoze kupirira zinthu zimenezo, umene ukufuulira? Kodi muli chinachake muno chimene chikundipangitsa ine ngakhale kumatsutsana ndi kaganizidwe kanga komwe, kufuna kwanga komwe?” Ine ndinati, “Ziripo zinthu zitatu zokha zomwe zingakhoze kukhala ziri. Izo zikhoza kukhala kuti mwina ine ndasokonezeka malingaliro anga. . .” Ngati ine ndiri, ine sindikuzidziwa izo. Ndine wamanjenje, munthu wokwiysidwa. Icho ndi chibadwa changa basi. Mphatso yanga imachititsa izo, koma, monga mtumiki. Koma i—i. . . “Ine mwina ndasokonezeka malingaliro anga, kapena ine ndasanduka wotentheka, kapena ndi Mzimu wa Mulungu.” I—izo ziyenera kukhala chimodzi cha zinthu zimenezo.

⁴⁵ Koma, ine sindingakhoze kupirira kumaziwona zinthu, ndi chinachake mkatimu chimangofuulira kunjja. Ndipo komabe ine ndikudziwa, molingana ndi Baibulo, kuti izo ziyenera kumachitika. Ndiye ndi ubwino wanji umachitika kuti ufuule? Mulungu adzaima bwanji pa Chiweruzo ndi kudzakaponya

kam'badwo aka kuno ngati Iye alibe liwu likufuulira motsutsa izo, kuti libweretse chiweruzo? Zikanati zidzakhale bwanji ndi Afarisi, ngati kukanati kusakhale Yohane akufuula kuchokera ku chipululu? Zidzachitira ubwino wanji, pamene ine ndiwauza, "Iwo asamachite *izi*, ndipo asamachite *izi*, ndipo asamachite *izi*, ndipo inu musati muzichita *izi*. Ndipo inu mukhale mutadzazidwa nawo Mzimu?"

Iwo amayenda pafupi nati, "Wasokonezeka mutu! Wapenga! Chinachake chachitika kwa iye!"

Chabwino, ndi cha ntchito yanji kuchita izo? Chifukwa, Mulungu ayenera kuti akhale nalo liwu. Liyenera kuti lizinena izo, mulimonse, chotero Iye akhoze kubweretsa chiweruzo, kudzati, "Ndi izo apo. Sindinu osadziwa izo." Ndiko kulondola. Ndipo ngati iwe sufuulira momveka, kodi Iye achita chiani? Pali chinachake chikufuulira kunjja, mwa iwe. Iwe sungakhoze kuziletsa izo.

⁴⁶ Tsopano, tsopano ife tikupezano, ndiye, kuti pamene ife tinabweretsa pansi chinthu chinacho chomwe ife tiri nacho pano, tikupeza, ku—kuti, chifukwa chomwe ife sitiri achipembedzo. Ndipo ife tikukhulupirira kuti alipo Akhristu obadwa kachiwiri, anthu oyera, mu Methodist, Baptist, Presbateria, Chipentekoste, ndi zina zonse. Ife tikukhulupirira kuti Mpingo wa Mulungu ndiwo Mbewu iyo yomwe yasakanizidwa kudutsa mu gawo ili podutsa pansi pano, ndipo iyo inabweramo ndi zomwe ife tinaziyanikhula usiku watha, ndipo ife tikambirana izo mopitirira, kukonzedweratu. Osati kuti Mulungu amakonzeratu chirichonse kuti chidzakhale chiri, koma, mwa kudziwiratu Iye akhoza kukonzeratu, pakuti Iye ankazidziwa zinthu zonse.

⁴⁷ Ndipo ife tinapeza usiku watha kuti palibe wina aliyense anayamba wapulumutsidwapo, monga usikuuno, ndipo anachititsa dzina lawo lilembedwe pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa. Dzina lanu mwina linaikidwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa dziko lisanayambe, kapena silinalipo uko kapena silidzakhala liripo. Ife tikupeza, pamene Mulungu anamupha Mwanawankhosa asanaikidwe maziko a dziko, inu munaphedwa ndi Mwanawankhosa wanu. Inu mukukhulupirira izo? Tizipeza miniti chabe.

⁴⁸ Tiyeni titembenezire ku Chivumbulutso, kuti tiyambire, Chivumbulutso 17 kapena... Chivumbulutso 13:8, ndipo tipeze apa zomwe Baibulo limanena za—za ngati... pamene Mwanawankhosa anaphedwa. Tiwone ngati Iye anaphedwa mu ad. 33, kapena ad. 33, kapena ngati Iye anaphedwa pati... pamene Iye anaphedwa. Chabwino. Tsopano, uyu ndi United States mu ulosi apa, inde. Tsopano ife tiweringa izi.

Ndipo onse okhala pa dziko lapansi adzamupembedza iye (Chiani? Chirombo.), omwe maina awo

*sanalembedwe mu bukhu la moyo wa Mwanawankhosa
wophedwa kuchokera ku maziko a dziko.*

⁴⁹ Ndi liti pamene Mwanawankhosa anaphedwa, zaka thuu sauzande zapitazo? Mwinamwake zaka handiredi milioni zapitazo. Maziko a dziko asanaikidwe konse, Yesu Khristu anafera machimo athu. O, koma tsopano ine ndikuyamba kukhala wachipembedzo. Kusanakhale konse dziko, Yesu Khristu anafa kuti alipulumutse ilo.

⁵⁰ “Chabwino,” inu mukuti, “ndiye nchifukwa chiani Mulungu, Mulungu wopanda malire, analiloleza konse tchimo?”

Inu mukudziwa, muli zikhumbo mwa Mulungu. Ndipo ngati Mulungu akanati asamuloleze Satana . . . Iye ankadziwa, pamene Iye ankamulenga Lucifara, kuti iye anali woti akhale yemwe akanadzaliyipitsa dziko. O, Mulungu wathu sali chinachake chaching’ono, chokankhidwira ku ngodya ina, koma Iye ndi Mulungu wopandamalire Yemwe sanayambe konse wakhalapo ndi chiyambi kapena sadzakhala nawo konse mapeto. Ndipo, mwa Iye, Iye ali mu zikhumbo Zake. Iye ndi Mpulumutsi. Ndipo Iye akanakhoza bwanji kudziwika konse monga Mpulumutsi ngati pakanati pasakhale chinachake choti achipulumutse? Ife tikanadziwa konse chotani . . .

⁵¹ Nchiani chinali choyamba? Ngati, ine nditafunsa funso. Nchiani chinali choyamba, Mpulumutsi kapena wochimwa? Chabwino, ngati Mpulumutsi anali woyamba, ndipo Mpulumutsi ndi wapamwamba kuposa wochimwa, nanga wochimwa anadzapezeka bwanji alipo? Ngati pakanati pasakhale wochimwa, iye sibwenzi atamudziwa Iye konse ngati Mpulumutsi. Nchiani chiri champhamvu kwambiri, mchiritsi kapena munthu wodwala? Wochiritsa amangowachotsa matendawo ndi kuwawononga iwo. Choyamba chinali chiani, Mulungu kapena khansara? Poti, analipo Mulungu, poyamba. Nchifukwa chiani Iye analoleza—matenda ndiye? Chifukwa, ngati Iye angakhoze kuwawononga iwo tsopano, Iye akanapangitsa iwo kuti asamachitike. Ndipo ngati Iye ali wopandamalire, Iye ankadziwa kuti zikanati zidzachitike. Komano, ngati Iye satero—ngati Iye satero, ngati pakanapanda kukhala matenda, ndiye Iye sakanati adziwike monga Mchiritsi. Koma pokhala kuti Iye ndi Mchiritsi, payenera kuti kukhale kuli matenda. Inu mukuona zomwe ine ndikutanthauza? Tsopano, Iye ankadziwa zinthu zonse.

⁵² Tsopano, mu Chivumbulutso 13:8, mvetserani. “Ndipo Mwanawankhosa anaphedwa” (Liti?) asanaikidwe “maziko a dziko.” Mulungu mu malingaliro Ake opandamalire, akuyang’ana pansu kudutsa mu mitsinje ya nthawi, ndipo Iye anawona zomwe zikanati zidzachitike, ndi momwe Iye akanati adzalengere ndi kudzagwera pansu mu danga ili la nthawi, kuti adzakokeremo zomwe Iye anali kwenikweni.

⁵³ Bwanji simuli inu aang’ono . . . inu amuna omwe muli nawo akazi anu, kuwaika akazanu pa yesero ndipo inu mungaone chomwe anapangidwa nacho. Ndiko kulondola. Kumuika mwamuna pa yesero, kugwedezera botolo pansu pa kamwa yake, ngati iye akhala ali chidakhwa. Izo zikuuzani inu ngati iye anapulumsidwa kwa izo kapena ayi. Ngati iye wakhala ali mthakati, woyenda yenda, garu wauve yemwe amaswa manyumba a amuna ena; muvuleni mkazi wina ndi kumuyamba iye . . . muyambeni naye iye, ndipo izo zikuuzani chomwe iye anapangidwira nacho. Ndiko kulondola. Ndithudi

⁵⁴ Mulungu, kuti asonyeze mphamvu Yake, kuti asonyeze chomwe Iye anali, kuti Iye anali Mpulumutsi, Iye anamulola wochimwa kuti akhalepo kuno.

⁵⁵ Monga ine ndanena, Angelo azidzaimba bwanji nkhani za chiwombolo, pamene iwo sakudziwa nkomwe chomwe chiwombolo chimatanthauza? Koma, ife tikhoza kuyimba iyo. Ife tikudziwa chomwe zimatanthauza kukhala utatayika ndi chomwe chimatanthauza kukhala utapezedwa. Iwe usanatayikepo konse, iwe sumadziwa chomwe chimatanthauza kukhala utapezedwa. Ndi iwo omwe anatayikapo, amadziwa chomwe chimatanthauza. Ndi iwo omwe anakhalapo ndi matenda, omwe amadziwa momwe ungasangalalire ndi thanzi labwino pamene ilo libwera. Ndi munthu woipa uja yemwe ankayenda mmisewu kutaliko, yemwe analibe konse bwenzi, ndipo analibe konse aliyense woti ayikepo mkono wawo momuyangata, ndipo analibe aliyense konse woti angayang’ane konse iwo ndi kuwalingalira iwo; ndi munthu ameneyo yemwe amadziwa chimene bwenzi lenileni amatanthauza, akati ayike mkono momukumbatira. Zedi, iwe umayenera kuti udziwe.

⁵⁶ Ife tikanadziwa bwanji kuyamikira kuwala kwa dzuwa ili, ngati pakanati pasakhale usiku? Inu mukanadziwa bwanji kuliyamikira tsiku labwino, lowala, ngati pakanati pasakhale lina lamitambo? Inu mukanadziwa bwanji kuyamikira kutentha kwa kuwala kwa dzuwa kwa mchirimwe, ngati pakanati pasakhale dzinja? Lamulo la zotsutsa ndi zovomereza. Ine ndikuyamba kuchoka, pa kulalikira. Ine sindimatanthauza kuti ndichite izo. Chabwino.

⁵⁷ Chivumbulutso 17:8, pamene ife, kwa miniti yokha tsopano, kuti tisonyeze tsopano. Mwanawankhosa anaphedwa liti? “Asanaikidwe maziko a dziko.” Chabwino. Chivumbulutso 17:8.

Ndipo chirombo chimene iwe unachiwona, chinalipo ndipo palibe; ndipo chidzatsikira ku dzenje lopandamalire, ndipo chidzapita ku chiwonongeko: ndipo iwo okhala pa dziko lapansi adzadabwa, omwe maina awo sanalembedwe mu bukhu la moyo kuchokera — bukhu la moyo kuchokera (liti?) ku maziko a dziko, . . .

58 Ndi liti pamene dzina lanu linayikidwa mu Bukhu la Moyo? Monga ine ndinanena usiku watha, munthu yemwe analemba nyimbo, “Pali dzina latsopano lalembedwa uko mu Ulemerero, ndipo ndi langa, ndi langa,” mwatanthauzo iye anali kulondola, koma Mwamalemba iye anali kulakwitsa. Dzina lanu silinalembedwe usiku umene inu munadza kwa Khristu.

Yesu anati, “Onse omwe Atate anandipatsa Ine adzadza kwa Ine. Ndipo palibe angakhoze kubwera kupatula Atate Anga atamukoka iye. Onse omwe adza kwa Ine, Ine ndidzawapatsa iwo Moyo Wamuyaya, ndipo ndidzawaukitsa iwo pa tsiku lotsiriza. Palibe wina wa iwo wotaika. Ine sinditaya kalikonse, chifukwa palibe munthu angawakhwathule iwo kuchokera mdzanja la Atate Anga. Yemwe anawapereka iwo kwa Ine.” O, mai! Pfyuu! Yohane Woyera 5:24, “Iye Yemwe amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya, ndipo sadzabwera konse ku chiweruzo, koma wadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo.” Ndicho chifukwa mpingo uno umakhulupirira mu chitetezo cha kupirira kwa oyer, osati mu kachitidwe ka Chibaptisti, osati mu kachitidwe ka Chipresbateria, koma mu kachitidwe ka Baibulo.

59 “Chabwino, inu mukuti, “tsopano, M’bale Branham, ine ndikulingalira kamodzi mu chisomo nthawizonse uli mu chisomo.” Izo zimabweretsa zopanda chisomo zochuluka. Koma pamene mwamuna kapena mkazi wabadwa mwa Mzimu wa Mulungu, zinthu zakale zapita, zinthu zonse zсандuka zatsopano, ndipo iye wabalidwa ndi kudalitsidwa ndi Mulungu Wamuyaya. Ndipo iwo sangakhoze konse kuwonongeka monga Mulungu Mwiniwake sangawonongeke.

60 Kodi inu mukutanthauza kuti mudiuze ine kuti Mulungu, Mulungu wopandamalire, akanabwera pansu ndi kukupatsani inu Moyo Wamuyaya, akudziwa kuti Iye akanati akutayeni inu? Kukupulumutsani inu pano, akudziwa kuti Iye akutayeni inu apo? Nanga anakupulumutsirani chiani inu? Ndiyetu, Iye akuchita modzitsutsa Iyeyekha. Ngati Iye anakupulumutsani inu kamodzi, ndinu wopulumutsidwa kwa Muyaya wonse. Palibe ziwanda mu gehena zingakhoze kukusokonezani inu.

61 Tsopano, Mulungu wopanda malire Yemwe akanakhoza kudziwa mapeto kuchokera kuchiyambi, ndiyeno nkukupulumutsani inu pano, sabata ino, ndipo akudziwa kuti chaka chamawa inu mudzabwerera mmbuyo, ndi kudzakutayeni inu? Chabwino, nchifukwa chiani Iye akuchita ntchito yonga imeneyo? Izo zikanakhala zopusa; ine sindikanachita izo. Ngati ine ndikanakupangani inu bwenzi langa lero, ndikudziwa kuti inu mukhala mdani wanga mawa, chabwino, ine sindikanachita izo. Ine ndikanangokusiyani inu nokha. Mwaona? Mulungu akukupangani inu wantchito Wake, lero, chifukwa Iye akudziwa, ndipo ankadziwa inu musanabwere konse pa dziko lapansi. Pamene Iye ankapanga kashiamu yemwe anapita mu thupi

lanu, pamene Iye anakalenga kuwala kwadziko kumene inu... komwe kuli mwa inu. Pamene zimafuta ndi zonse zomwe inu munapangidwa nazo, pamene Mulungu anakazilenga izo pa dziko lapansi, Iye anakadziwa msempha uliwonse wa inu ndi chomwe inu mukanati mudzachite. Angakhoze bwanji Mulungu wopandamalire...

⁶² “Chabwino, ine kulibwino ndiyende mosamala lero; ine mwina ndikhoza kubwerera mmbuyo ndi kudzatayika mawa.” Inu simunapulumsidwe poyamba pomwe. Inu mukhoza kukhala mutangotengeka, pansi pa zotengeka. Inu mukhoza kumangoganiza kuti inu munapulumsidwa. Inu mukhoza kumamverera ngati munapulumsidwa. Inu mukhoza kumakhulupirira kuti ndinu opulumsidwa. Inu mukhoza kujowina mpingo. Inu mukhoza kukhala wa Baptisti wabwino, wa Methodisti, kapena Wachipentekoste. Izo ziribe chinthu chimodzi chochita nazo. Dzina lanu liri konse... Ngati inu munapulumsidwapo konse, inu munapulumsidwa dziko lisanayambe konse, pamene Mulungu anatumiza Yesu, mu malingaliro Ake, kuti adzamupulumutse uyo yemwe Iye anamuwona kuti angapulumsike. Tsopano, Iye sali kulolera kuti wina atayike. Iye sali kulolera, koma, ngati Iye ali Mulungu, Iye anamdziwa yemwe akanati ndi yemwe sakanati adzatero. Lemba limanena chomwecho. Chotero ndi inu apo.

⁶³ Ndi chifukwa ife timasiyana ndi a Baptisti, Amethodisti, ndi anthu otchedwa oganiza mwachi Kalvini. Koma, Chikalvini ndi cholondola.

⁶⁴ Ndiye ife tipita kufika cha kumbali ya chi Armeniani. Kodi iwo anapeza chiani? Zintchito. Ndilo gulu lachiyero. Zintchito, “Adalitsidwe Mulungu, ine ndililola tsitsi langa lizikula,” akazi. Ndipo, “O, Mulungu alemekezeke, ine sindimavala konse malaya a gwanda,” mwamuna kutero, ndi zina zotero zonga izo. Izo ziribe kanthu kochita ndi Ufumu. Ayi, bwana. Inu mukhoza kulola tsitsi lanu likule motalika, inu mukhoza kumavala madiresi paliponse pomwe inu mukufuna kutero, kapena inu mukhoza kuchita *izi, izo*, kapena *zinazo*, ndipo izo sizidzakhala konse ndi kanthu kochita nazo. Inu simunapulumsidwe chifukwa cha zovala zanu. Ngati ziri choncho, Mulungu akanangopanga mapatani ena a zoterozo. Yesu sakanasowa kuti afe.

Inu munapulumsidwa chifukwa chakuti Mulungu anakupulumutsani inu, mwa chisomo, ndipo inu mumachita zinthu izi pongoyamikira. Makhalidwe wamba angakuuzeni inu zimenezo. Inu mumachita zinthu izo poyamikira. Ntchito ndi zomwe ine ndimamuchitira Mulungu.

⁶⁵ Ngati ine sindikanalalikira konse ulaliki wina, ndi kukhala moyo kuno zaka handiredi ndi fifite, ine ndikanali wopulumutsidwa. Zedi. Ine sindiri wopulumutsidwa chifukwa ndine mlaliki. Ine ndinapulumsidwa chifukwa ndi chisomo

cha Mulungu chimene chinandipulumutsa ine. Panalibe chinthu chimodzi chimene ine ndikanakhoza kuchita kuti ndiyenere izo.

⁶⁶ Ine ndasumiridwa ndi lamulo, pakali pano, chifukwa cha madola theka la milioni. Ndipo iwo akuti, “Bwanji, iwe unapita uko. . . Ndalama izo zomwe iwe unakatenga uko, kuti ulipire ngongole zako. Izo zinali zako iwe usanalipire ngongole zako. Iwe unazidutsitsa izo mu tchalitchi chako, koma izo zinali zako poyamba.”

Ine ndinati, “Koma ine sindinachite kanthu kamodzi kake.”

Anati, “Inde, iwe unachita,” anati, “iwe unawauza iwo kuti iwe utenga chopereka chachikondi.”

Ine ndinati, “Ine ndikufuna wina andiuze ine pamene izo zinali.”

Chabwino, iwe unkapempha kudzera mmakalata?”

Ine ndinati, “Kafufuzeni ofesi yanga; palibe tambala.”

⁶⁷ Inu mukudziwa, Baibulo linati, “Musati muzitenga lingaliro pa zoti mukanene, pakuti izo zikapatsidwa kwa inu mu ora limenelo.” Ndipo ndinali nditakhala apo pafupi ndi oweruza mlandu aboma awo, ndi aliyense akuzaziranso kwa ine, kuchokera mbali imodzi ndi ku inayo; ndipo ine wosadziwa nkomwe ma ABC anga. Ndipo ndi amuna anzeru awo omwe ali ophunzitsidwa kuti akupangitse iwe kuti unene zinthu zomwe iwe sumatanthauza kwenikweni kuti uzinene izo, ndiye iwe ungangizifanizitse nzeru chotani ndi winawake wonga uyo? Iye sangakhoze konse kufanana nzeru ndi Mbuye wanga, ngakhale. Lemba ili linati, “Musati muziganizira ayi pamene inu mubweretsedwa pamaso pa mafumu ndi olamulira.”

Ine ndikudziwa ndalama zomwe ine ndinakatenga uko, ine ndinazigwiritsa ntchito izo. . . Ndipo iwo sanatsutse izo. Izo zinali zitagwiritsidwa ntchito mwa njira yake monga izo zikanakhoza kugwiritsidwira. Koma iwo anati, “Izo zinali zako, poyamba, ndiyeno iwe unazisandutsa izo kukhala za Branham Tabernacle.”

Ine ndinati, “Koma ndine msungichuma wa Branham Tabernacle.” Ndipo izi. . .

Chabwino, iye anati, “Ine sindikudziwa za izo. Ndiye nchifukwa chiani matrasti sanachite izi, izo, ndi zinazo?” Wina. . .

Ine ndinati, “Ndiye inu mukunditcha ine wosawona mtima?”

⁶⁸ Anati, “Ife tikuganiza ndinu owonamtima kwambiri.” Anati, “Ine ndikufuna ndikusonyezeni inu chinachake, Bambo Branham,” woweruza mlandu uyo.

Ine ndikungonena izi kwa ulemerero wa Mulungu tsopano, kokha, ndi makamaka chifukwa cha aang’ono. Iye anati,

“Ine ndikufuna kuti ndikusonyezeni inu chinachake, kuti ndikusonyezeni inu momwe. . .” Ngati inu muzikhala moyo ndi Baibulo, Mulungu azikhala moyo ndi inu. Ndipo ngati mzimu wanu uzitsutsana ndi zomwe Mulungu ananena, ndiye inu simukukhala moyo ndi Baibulo.

⁶⁹ Kumbukirani usiku watha pamene ife timakamba za alaliki achikazi, pamene iwo ati, “O, ine ndikukhulupirira Mzimu Woyera unandiyitana ine kuti ndizikalalikira,” ndi zina zotero monga choncho? Baibulo linati, “Ngati munthu wina anena kuti iye ali mneneri, kapena ngakhale wauzimu, muloleni iye azindikire kuti Izi ndi malamulo a Ambuye; koma ngati iye ali wosazindikira, ingomusiyani iye akhale wosazindikira.” Chotero pamene inu muwamva anthu akunena kuti iwo amakhulupirira alaliki achikazi, izo zimasonyeza kuti iwo sali mwabwino ndi Mulungu, kapena sakudziwa Choonadi. Ndicho Choonadi. Lemba limanena chomwecho. Ife tinazipeza izo Umo, ndipo zikungogwirizana kudutsa mu Malemba. Tsopano, ziribe kanthu momwe zikuwoneka ngati zenizeni chotani, ndi zosiyana. Si zolondola.

⁷⁰ Tsopano, ife titenga chinachake pano tsopano. Zindikirani. Mulungu, Mulungu wopanda malire, Yemwe anapanga dziko lapansi, ndi miyamba, ndipo ankadziwa zinthu zonse, ndipo anazidziwa izo dziko lisanaumbidwe nkomwe, utitiri uliwonse, ntchentche iliyonse, tongole aliyense, chirichonse chomwe chikanati chidzakhalepo. Ndipo inu muzikhala moyo ndi Mawu Ake.

⁷¹ Ndiye, nditaima apo pafupi ndi oweruza mlandu awo. Woweruza mlandu uyu anabwera apo nati, “Ife sitiri, mwanjira iliyonse, kuyesera kunena kuti ndinu wosaoona mtima.” Anati, “Inu simumadziwa pa zoonza zakuti pamene aliyense akupatsani inu ndalama izo zinali zanu poyamba.” Anati, “Inu munasaina cheke chochokera kwa Bambo Miner Arganbright, aku—a ku California, a Christian Business Men’s Full Gospel Fellowship, cha madola ochulukika zikwi *chotero*. Ndipo tsiku lomwelo inu munazitenga izo mu banki yanu ndipo munagula matikiti anai kapena asanu a ulendo waku tsidya kwa nyanja, pafupi madola twente-foro sauzande.”

Ndinati, “Inde, bwana.”

Iye anati, “Inu muli ndi ngongole ya msonkho pa izo.”

Chifukwa, ine ndinati, “Ife tinali titaima mu banki yomweyo, ndipo iye anandipatsa ine chekecho, ndipo ine ndinachidutsitsa icho mu banki ndi kulemba matikiti mowabwezera pomwepo.”

Iye anati, “Ngati inu munakhala nacho chekecho miniti imodzi,” anati, “theka la izo, zinali zanu. Inu munakhala nacho icho, theka la miniti. Izo zinali zanu, theka la miniti, izo

zisanakhale chuma cha mpingo.” Anati, “Inu muli ndi ngongole ya msonkho pa izo.”

Anati, “Iye anzipereka izo kwa mpingo. Iye analipira msonkho pa izo, ndipo iye anapereka izo kwa mpingo. Iye anzipereka izo kwa inu.”

Ndipo ine ndinati, “Iwe umalipira msonkho pa izo, izo zimapita ku mpingo, ndiye nzosalipiridwa msonkho.”

Anati, “Ife sitikulipiritsa msonkho mpingo wanu. Ife tikulipiritsa msonkho inuyo.”

Ine ndinati, ndiye, “Poti,” ine ndinati, “munthu yemweyo amene anasaina dzina lake, pa msonkho wa boma, anandiuza ine kuti ndizichita izi mwanjira iyi.”

Iye anati, “Iye sali ndi boma panonso.”

Ine ndinati, “Iwo amene analemba Malamulo salinso ndi boma panonso, kodi iwo akuimabe? Ine ndinati, “Tsiku lina inu simudzakhala muli ndi boma aponso, ndipo nanga mukunena chiani ndiye?” Ine ndinati, “Kodi ife tikutumikira boma la mtundu wanji?” Ndithudi.

Koma, ndiye, ndipo munthu winayo anati, “Bambo Branham,” iye anati, “ife tikupeza pano, mundilore ine ndikusonyezeni inu kumene ndalama iliyonse yomwe inu mumaigwiritsa ntchito ili.”

Ine ndinati, “Chabwino.”

Iye anati, “Apa pali malo omwe inu munkachititsa msonkhano mu Canada, mu Alberta, ndipo kumeneko inu munapatsidwa chopereka cha chikondi cha madola zikwi zitatu.”

Ine ndinati, “Inde, bwana.”

Ndipo anati, “Lotsatira . . . Lamlungu lapitalo, kani, kwa ilo, inu munapita ndipo munakapeza kumene kunali tchalitchi chakale, ndipo iwo anali akupembedzera mu tchalitchi ichi, ndipo chinalibe denga pa icho. Ndipo inu munapereka madola firii sauzandewo kwa anthu awo, kuti amangire tchalitchi.”

Ine ndinati, “Ndiko kulondola.”

Anati, “Koma inu muli ndi ngongole ya msonkho pa izo.” Anati, “Inuyo munazipereka izo kwa mpingo.” Anati, “Mwaona, izo zinali zanu izo zisanakhale za mpingo.”

Iye anati, “Kodi izo si zoonza, kuti bambo *winawake* . . .” Ndipo ine sindimutchula dzina lake, chifukwa ambiri a inu mukumudziwa iye. “Nyumba yake inapsya, kuno mu dziko, ndipo inu munali mutabwera, kuchokera ku msonkhano wanu, ndipo inu munali ndi madola fifitini handiredi.” Tsopano, izo zikhoza kumveka ngati ndalama zochulukira kwambiri, kwa wina wa inu nonse. Koma awo ndi basi masiku fifitini kuti ine ndizilova, kapena kupumula. Zimanditengera ine kupitirira

madola handiredi pa tsiku, ngakhale ine ndizilalikira kapena ine ndisatero, kuti ndisamalire za ofesi ndi zina. Ndipo anati, “Inu munali ndi madola fifitini handiredi. Ndipo bambo ameneyo anali . . . nyumba inapsyeratu. Iye anali ndi pafupi ana sikisi, ndipo inu munamupatsa iye madola fifitini handiredi amenewo.” Zedi, iwo anali ndi cheke changa chiri apo.

Ine ndinati, “Uko nkulondola.” Ine ndinati, “Inu mukanachita chiani, bambo wa ana asanu akukhala mu hema, ndipo kukuzizira ndi chisanu pansi? Inu mukuganiza ine ndikanamakhalala mu nyumba yabwino ndi kumadziwa kuti bambo uyo ndi ana aang’ono awo kunja uko, akukongwa, ndi zikhoto ataziunjikira pa iwo, ndipo ndiri ndi ndalama zokhoza kumuthandizira iye?”

Iye anati, “Kodi si zoona kuti bambo anafa mu ngalande kumtunda kuno? Ndipo iye amachokera ku Kentucky. Iye analibe ngakhale ndalama zochitira mwambo wa maliro ake, ndipo inu munakamuika munthuyo. Ndipo inu ndi akazi anu munatenga ndalama ndipo munapita ku J.C. Penney.” Anafutukula machekewo. Anati, “Inu munawononga kupitirira madola thuu handiredi basi chifukwa cha zovala za ana amenewo.”

Ine ndinati, “Uko nkulondola.”

Iye anati, “Kodi si zoona kuti mayi wachikulire momwe muno mu mzinda *winawake* . . .” Yemwe ankakhala muno, pamenepo, New Albany. Ndipo anati, “Inu munampatsa iye madola firii handiredi ndi chinachake, kuti alipirire ngongole ya zaku golosale, yomwe, iwo anamuimisa nayo iye. Ndipo inu munalipira pafupi madola faifi handiredi pa lendi yake, yomwe iwo ankati amutulutsemo iye mu chisanu. Ndipo inu munalipira lendi ya—yake mpaka mu Juni wotsatira, ndiponso munamuimira bwino pa ngongole yake ya ku golosale yomwe inafika mpaka madola fortini kapena fifitini handiredi aponso.”

Ine ndinati, “Ine ndikuikumbukira nkhaniyo bwinobwino. Mayi wachikulire, wa usinkhu zaka eyite, ali ndi mwana wamkazi wosautsika, ndi mnyamata wolalikira ku Georgia, atasautsika ndi nyamakazi, ndipo atagona pa kama, ali wopanda thandizo lina lililonse. Inu mukanachita chiani pa izo?” Ine ndinati, “Inde, ine ndinatero.”

Anati, “Kodi gulu lanu la matrasti linadziwa izi?”

Ine ndinati, “Ayi, bwana, iwo sanazidziwe?”

“Kodi akazi anu ankadziwa izi?”

Ine ndinati, “Ayi, bwana, iwo sanazidziwe.”

Anati, “Ndiye nchifukwa chiani inu munkachita izo?”

⁷² Ine ndinati, “Chifukwa Ambuye anga anati, ‘Musati muzilora dzanja lanu lamanzere lizidziwa chomwe dzanja lanu

lamanja likuchita.” Ine ndinati, “Kodi muli nalo lamulo lirilonse lapamwamba kuposa malamulo a Mulungu?”

Ndipo basi apo Mzimu Woyera unabwera kudzandiwombola, mokongola kwambiri momwe Iye amachitira izo. Iwe umanena zinthu, mosaganizira, osadziwa kuti iwe ukuzinena izo, ngati iwe utangoulola Mzimu Woyera kuti uzichita kuyankhulako.

Ine ndinati, “Chabwino, chabwino, ngati inu mukunena kuti ine ndiri ndi ngongole iyo,” ine ndinati, “ine ndichita zopambana zomwe ine ndingathe.” Ine ndinati, “Ine sindine mnyamata panonso ayi, koma ine ndichita zopambana kuti ndiilipire iyo.” Ine ndinati, “Usamakhale ndi ngongole kwa aliyense, momwe ine ndikudziwira.” Ine ndayesera kukhala woona mtima. Ine ndinafika zikwi za madola mu ngongole, ndi kumabweza izo dola pa sabata. Koma, mwa chisomo cha Mulungu, ine ndinailipira iyo. Ine ndinati, “Ngati inu mukunena ndi kutsimikizira kwa ine kuti ine ndiri ndi ngongole ya ndalama izo zimene ine ndinawapatsa anthu amenewo. . .” Ndipo iwo anapitirira kumasonyeza pamene ziri pafupi madola twente sauzande, mu zaka khumi zapitazi, ine ndinapereka kwa ena monga choncho.

Ndipo iye anati, “Matrasti sankadziwa kanthu za izi.”

Ine ndinati, “Izo si zinali zofunikira kuti iwo azidziwe izo.” Ndipo kotero iye anati. . . Chabwino, ndiye iye anati. . .

⁷³ Ine ndinati, “Chimene chikundipweteka ine, ndi kudziwa kuti akazi amasiye ndi ana amasiye osauka achikulire awo, akasowa kuti akalipire msonkho pa izo, nawonso, kapena azifa, ali ndi ngongole kwa boma.” Ine sindinkadziwa zomwe ine ndinkanena. Awo anali Atate akuyankhula, ndipo ine sindinkadziwa izo.

“O,” iye anati, “ayi, iwo sakusowa kuti akalipire msonkho pa izo.”

Ine ndinati, “Bwanji kuti iwo asakalipire izo?”

Anati, “Inu mukuona, iyo inali mphatso yosachita kupempha.”

Ndiye Mzimu Woyera unandidzutsa ine. “O,” ine ndinati, “ndiye mphatso yosachita kupempha siimalipiridwa msonkho?”

Anati, “Uko nkulondola.”

Ine ndinati, “Ndiye ine ndiribe ngongole iliyonse kwa boma, pakuti ine sindinayambe ndatengapo chopereka mu moyo wanga.”

Ndiye woyimira mlandu wanga anauka, ndipo iye anati, “Bambo Branham mungakhoze inu. . .”

Ine ndinati, “Ine ndikhoza kukubweretserani inu makalata mamilioni awiri mu Washington, kuti nditsimikizire izo.” Ine ndinati, “Ine sindinatengapo konse chopereka.”

Anati, “Koma pamene inu mumapita mu misonkhano iyi, ndi ndalama izi zomwe zimatengedwa ndi atumiki awa ndi kumalipirira izi,” anati, “inu mumakhala ndi kumvetisa kwa mtundu wina kuti mupezapo chinachake.”

Ine ndinati, “Osati kanthu.”

Iye anati, “Ndiye, chabwino, inu simumapempha kupyolera mmakalata?”

Ine ndinati, “Osati kanthu.”

Anati, “Inu mumazipeza bwanji ndalama zanu?”

⁷⁴ Ine ndinati, “Zomwe anthu amanditumizira ine.” Ine ndikuyang’ana mmaso mwa anthu pakali pano omwe amanditumizira ine chakhumi mosalekeza. Ine sindinawapempho konse iwo. Iwo amangochita izo. Ndiwo Mzimu Woyera. Iye ndi wokhoza kuwasamalira Ake omwe.

Ndipo iye anati, “Chabwino, ndiye, Bambo Branham,” anati, “kodi inu mungatsimikizire izo? Inu mungakhoze kunditengera ine makalata a pafupi zaka eyiti kapena teni mmbuyo kuti inu mumalandira chopereka popanda kupempha?”

Ine ndinati, “Ochuluka momwe inu mungafunire.”

Iye anati, “Ine ndikufuna atatu pa chaka chirichonse.”

Ine ndinati, “Chabwino, inu mukhala nawo iwo.”

Anati, “Ndiye inu mungandipatse ine makiyi anu aku positi ofesi, ndi kundilola ine. . . Mulole makalata anu adzazane kwa masiku awiri kapena atatu, ndiyeno ndidzapite uko ndi kukatsegula iyo, inendekha?”

Ndinati, “Inu mukhoza kuchita chirichonse chimene inu mukuchifuna. Inu mukhoza kubwera ku ofesi yanga nakonso.”

Iye anati, “Ndi kupemphetsa kwa mtundu wanji kumene inu mumakuchita?”

Ine ndinati, “Palibe.”

“Inu mumatumiza chiani mu makalata?”

“Nsalu za pemphero.”

“Kodi inu mumalipiritsa izo?”

⁷⁵ Ine ndinati, “Mubwere, mudzawerenge makalata omwe ine ndimatumiza nazo.” Izo zinali choncho. Tsopano boma liri ndi ngongole kwa ine pa zonse zomwe ine ndimalipira, msonkho kwa boma, wa zaka twente zapitazi.

“Musati muzitenga lingaliro pa zomwe muti mukanene, chifukwa si inu yemwe mumayankhula pakuti ndi Atate amene ali mwa inu amachita kuyankhulako.” Mwaona? Ndi chifukwa chake ife timakhulupirira mu kukhala ndi Mawu. Izo mwina zikhoza kukhala nthawi yaitali, koma izo zidzagwira ntchito bwino basi, molingana ndi Mawu.

⁷⁶ Tsopano, ndicho chifukwa ife timakhulupirira kuti Baibulo limatiuza ife kuti dziko lisanawumbidwe nkomwe, ndipo lisanakhalepo konse, kuti Atate anapha Mwanawankhosa. Ndiyeno pamene Iye anamupha Mwanawankhosa, Iye anaika dzina la mwana Wake aliyense wakudza mtsogolo mu Bukhu la Moyo, ndipo ife timangokhala moyo ku m'badwo umenewo mpaka izo zonse zitatha. Inu mukuona zomwe ine ndikutanthaza? Mulungu wopanda malire ankadziwa izo, kuti dziko lisanayambe Iye anawona dongosolo la zomwe zinkati zidzachitidwe, ndipo Iye anangozikonza izo.

⁷⁷ Tsopano kumbukirani, monga Mbuye Womanga wamkulu, Atate, pamene Iye anapanga dziko lino ndi kuikamo kashiamu, potashi, ndi petroleamu, ndi zipangizo zonse zosiyana izi zomwe zimapitamo kuti apange matupi athu, Iye anadziwa chidutswa chirichonse cha izo ndipo anadziwa mtundu wake wa thupi lomwe akanati adzakhale nalo lisanalengedwe nkomwe. Ndithudi. Iye anawadziwa mapeto Amuyaya a izo. Ndipo Iye ankadziwa mtundu wa mizimu yomwe ikanadzakhala mwa iwowa.

⁷⁸ Ndipo tsopano, ife tisanati titsirize phunziro limenelo, ife tiyenera kuti tilitengenso usikuuno, mu “mbewu ya serpenti” ndi mu “mbewu ya mkazi,” ndi kuzitsitsa izo pansi ndi kukusonyezani inu chifukwa chomwe izo ziri. Kuona momwe mbewu ya serpenti inasunthira pansi, momwe mbewu iyo ya mkazi inasunthira pansi; momwe kuti mbewu ya serpenti inayamba kulamulira, lamulira, kumakula, ndi kukulira, kulira, kulira, kulira, mpaka tsopano palibe chimene chatsalira koma maina otsalira apang'ono ochepa omwe alipobe, analembedwa kuchokera ku maziko a dziko.

⁷⁹ Koma pamene Thupi laumbidwa, ndipo dzina lotsiriza ilo lomwe liri pa Bukhu lidzazindikiridwa pano pa dziko lapansi, Mabuku adzatsekedwa, pakuti iwo atsirizidwa, nkhani ya chiwombolo yawerengedwa kwathunthu. Ndiye ife tidzapita kukamuwona Iye ndi kukakomana naye Iye mu chiwukitsiro. “Iye amene amva mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya ndipo sadzabwera konse ku Chiweruzo, koma wadutsa kuchokera ku imfa napita ku Moyo.”

“Palibe munthu angakhoze kudza kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka iye.” “Ndipo si iye amene afuna kapena iye amene athamanga; ndi Mulungu yemwe amasonyeza chifundo,” linatero Lemba.

Si iye amene afuna. Anthu ambiri amati, “Ine ndijowina mpingo. Ine ndikufuna kuti ndikhale mnyamata wabwino. Ine ndizichita *izi*.” Izo ziribe kanthu kochita nazo izo. Ndi Mulungu yemwe amasonyeza chifundo.

⁸⁰ Tsopano, inu mukuona, pamene Mulungu anayamba, mu...Iliipo Mizimu seveni ya Mulungu, chimodzimodzi monga mitundu seveni mu utawaleza. Ndipo kodi inu munayamba mwazindikira? Chidutswa cha galasi cha ngodya zitatu chimanyezimiritsa mitundu seveni yangwiro. Kodi inu munayamba mwayeserapo izo? Mudzaike chidutswa cha galasi cha mbali zitatu; komabe chiri chidutswa chimodzi cha galasi, koma, mu ngodya zitatu, limanyezimiritsa mitundu seveni. Ndi momwe Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, pokhala Mmodzi, komabe amanyezimiritsa zikhumbo seveni zauzimu za Mulungu.

⁸¹ Ndipo, ndiye, Mzimu woyamba waukulu wa Mulungu, umene uli chikondi. Mulungu, monga utawaleza waukulu. Ife sitikanakhoza kulingalira momwe Iye amawonekera. Koma basi kungoti Iye amawoneka monga utawaleza, Mizimu iyo. Mzimu wangwiro wa chikondi, *wofira*. *Buluu*, Mzimu wangwiro wa chiyanjano. Basi Mizimu yonse yangwiro iyo! Ndiyeno iyo imayamba kumatsika, kumabwera pansu. Ndipo iyo imabwera njira yonse pansu kuchokera ku—chikondi cha *fileo* kapena... chikondi cha *Agapao*, kwa chikondi cha *fileo*, ndipo mpaka pansu ku kusilira, ndi kutsikira kwa chotsikitsitsa.

Ndiyeno Mulungu Iyemwini anadzakhala Mwamuna, Yesu, ndipo anatsika mwanjira yomweyo, mpaka ku maenje otsikitsitsa a gehena, ndipo anakatengamo iwo omwe Iye ankawadziwa asanaikidwe maziko a dziko, amene maina awo analembedwa mu Bukhu, ndipo anawaombola iwo kuti abwerere kwa Iyemwini. Ndi inu apo. Nkhani ya chiwombolo siingakhoze kudziwika kwathunthu mpaka ife titadzamuwona Iye ndipo ife titaima mwa kufanana Naye.

⁸² Tsopano, ndicho chifukwa ife sitiri chipembedzo. Ndicho chifukwa ife sitima-. . . Ife timayanjana mu kusuntha kulikonse kumene ife tingakhoze, kwa Mulungu. Koma ndicho chifukwa ife sitiri chipembedzo. Tsopano, kunjira kwa chipembedzo kumabwera zinthu zabodza izo.

⁸³ Tsopano, monga ine ndinanena, ine ndikukhoma zolimba, chifukwa ine ndikufuna kuti izo zikanirire. Tsopano, kutali uko, mu mpingo wa munthu wina, ine sindikanati ndiganize za zinthu izi. Ine ndikanakhala Mkristu ndi m'bale mokwanira kuti ndingokhala pa mfundo zazikulu zomwe ife tonse timagwirizanapo. Mwaona? Koma, ndizo basi—ndizo basi monga, ife sitikufuna kumanamiza.

⁸⁴ Ine ndinali kuyankhula kwa mnyamata dzulo, kumene ine ndinali kusaka agologolo, dzulo mmawa, kutali komwe mu mapiri a Kentucky. Ndipo ine sindinachizindikire chikwangwani chokhomedwa mu mitengo, ndipo ine ndinali nditakhala ku mbali inayo. Ndipo ine ndimaganiza kuti anali M'bale Banks kuno, anabwera kudutsa mu nkhalangoyo. Iye anali akusaka agologolo, aponso, mu dera lomwelo. Ndipo ine

ndinamuwona iye akubwera, ndipo ine ndinamulizira likhweru mnyamatayo. Ine ndinkaganiza kuti anali M'bale Woods, atavala chimodzimidzi monga iye. Iye anatembenuka apo, ndipo ine ndinawona kuti sanali iyeyo.

Ndipo M'bale Woods anali atandiuza ine kuti kunali malo uko omwe anaikidwa chizindikiro. Ndipo ine sindinali kuwadziwa iwo. Kunalibe zingwe za mipanda; nkhalango basi. Ndipo ine ndikanadzadziwa bwanji kuti ndi mtengo wa mgwalangwa uti uli waku mbali iti? Chotero ine ndinali nditakhala pamenepo ndikumvetsera kwa gologolo akukuwa. Ndipo ine ndinali kuganiza zoti, "Chabwino, tsopano, usikuuno ine ndipita kunyumba ndi kukayamba msonkhano. Ine ndikabwerera mu ntchito kachiwiri." Ndipo uko kunayamba kuvumba, ndi mikuntho ikuwomba.

⁸⁵ Ndipo ine ndinamuwona munthu uyu, ndipo ine ndinayankhula kwa iye. Ndinapita komweko ndipo ndinakapeza kuti ine ndinali ku malo ake. Mwaona? Ndipo ine ndinayankhula kwa iye. Iye anati, "O, ziri bwino." Iye anati, "Mai, zingosakani kulikonse kumene inu mukufuna." Ndipo ine ndinati, chabwino. . . Iye anati, "Inu simunali ku malo anga. Inu munali mutakhala kupitirira mtengo wa mgwalangwa uwo." Anati, "Kumbali ino ya mtengo wa mgwalangwa ndiwo malo anga. Koma," anati, "izo ziribe kanthu, M'bale Branham. Zisakani kulikonse kumene inu mukufuna. Mubwere mpaka ku nyumba. Bambo akanafuna kuti akuwoneni inu." Mwaona? Ndipo ine ndinati, "Chabwino. . ."

Ife tinayamba kuyankhula za Baibulo. Ndiye tinapitirira pa phunziro losaka, iye ananena izi, iye anati, "M'bale Branham, palibe wina aliyense kuno amasamala za winawake kuti akusaka. Koma," anati, "bambo anga anali kuno tsiku lina ndipo wina wosaka wa mu mzinda anatulukira ndipo anadzapha imodzi ya nkhosa zake yomwe inkalempera pafupi mapaundi sikisite kapena sevente, ndipo iye anafuulira kwa munthuyo, ndipo munthuyo anamuwombera iye, ndi mfuti." Iye anati, "Ndizo zomwe zimapangitsa izo kukhala zoyipa." Anati, "Ife sitisamala za kusaka."

⁸⁶ Chabwino, ndi chinthu chomwecho chimene ine ndikuchikamba. Ine ndiribe nazo ntchito chipembedzo chomwe inu mulimo, koma khalani ndi Baibulo ndi Mzimu Woyera. Si chipembedzo chanu chimene ife tiri kudandaula nacho; mwamsanga khalani basi wa china monga wa chinacho. Koma, kuli kukhala ndi Baibulo kapena kulandira mbalume zopangidwa ndi anthu. Khalani ndi Baibulo.

⁸⁷ Tsopano, iwo anabweretsapo chipembedzo, chimene chinali cholakwika. Tsopano, chinthu chotsatira chimene iwo anachibweretsapo, chimene chinali cholakwika, chinali ubatizo wa madzi. Ubatizo wa madzi, monga zaphunzitsidwira mu Baibulo, ndi mwa kumiza. Koma mpingo wa Katolika

unabweretsapo kukonkha kapena kutsanulira. Ndipo palibe Lemba lina mu Baibulo lovomereza za kukonkha kapena kutsanulira; palibe malo oterowo amapezeka mu Baibulo. Ndi mwa kumiza.

⁸⁸ Chabwino, ndiye, koma motsatira apo kunadza, utatha mpingo wa Katolika, ndi mpingo wa Lutera, ndi kutsanulira kwawo. Ndipo motsatira kunadza mpingo wa Anglikani, ndi ina yotero, pamene iyo imadzapo.

Ndiye, patapita kanthawi, Achibaptisti anabweramo ndi achi Campbell, kuti abwererenso ku kumiza kachiwiri. Chabwino, Satana anachiwona icho, kotero basi iye anangowapatsa iwo dzina labodza kuti azimizidwiramo. Ndipo iwo anayamba kugwiritsa ntchito Dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi Mzimu Woyera. Palibe chidutswa chimodzi cha Lemba mu Baibulo pamene aliyense anayamba wabatizidwapo mu dzina la “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” Ndipo yense yemwe angamaphunzitse izo ndi mphunzitsi wabodza. Ndipo ine ndinakuuzani inu ine ndizipangitsa kuti zikanirire.

⁸⁹ Tsopano, ngati inu simukuganiza kuti uko nkulondola, ine ndikufuna funso lanu pa nsanja pano, mundisonyeza ine. Ngati inu mungakhoze kundisonyeza ine malo amodzi pamene aliyense anayamba wabatizidwapo, mu Baibulo, mu dzina la “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,” ine ndiyika chikwangwani pa nsana wanga, ngati “mphunzitsi wabodza,” ndi kumakwera-ndi-kutsika msewu, ndikufuula pamwamba pa mawu anga, ndi manja anga mmwamba, “Mphunzitsi wabodza!”

Palibe chinthu choterocho. Kodi icho chinachokera kuti? Tsopano bwererani mmbuyo. Iyi ndi mbali ino ya Baibulo. Inu muyenera kutenga mbiriyakale. Achikatolika amakhulupirira mwa amulungu ambiri, ndipo iwo anamuswa Mulungu mmodzi woona kukhala amulungu atatu osiyana.

⁹⁰ Ndipo ndimvereni ine. Chinthu choyipa chake chomwe chinali mu pepala tsiku lina, chokhudza munthu wamkulu yemwe ife tonse tikumudziwa kuti ali wantchito wa Mulungu; Billy Graham. Ife tiri nazo zonedwazo. M'bale Beeler, apo, ali nazo izo. Pamene anafunsidwa, Billy Graham, ndi *winawake*, “Yemwe, kunali chiani kutsutsana uku kokhudza utatu? Kodi kunali amulungu atatu, amulungu atatu enieni? Kapena, kodi izo zinali motani? Malo amodzi, iwo amawoneka ngati amulungu atatu. Ndipo ena amawoneka ngati ali pa- . . .” Billy Graham anati, “Izo sizinaululidwebe. Palibe yemwe akuzidziwa.” Mai!

⁹¹ Ngati alipo amulungu atatu, ndife achikunja. Monga Myuda anati, “Ndi uti wa iwo ali mulungu wanu? Atate? Kodi Mwana ndiye Mulungu wanu? Kapena, kodi Mzimu Woyera ndiye Mulungu wanu?” Pali Mulungu mmodzi yekha.

Ndipo awo si umunthu utatu, pakuti umunthu uyenera kukhala wa munthu. Izo sizingakhoze kukhala umunthu

popanda kukhalapo munthu. Inu mukudziwa izo. Kodi chirichonse chingakhoze bwanji kukhala umunthu mopanda kukhala munthu?

⁹² “O,” anati, “ife sitimakhulupirira mu amulungu atatu okhala anthu. Ife timakhulupirira mu umunthu utatu wa Mulungu yemweyo.” Chabwino, izo zisanakhale umunthu, izo ziyenera kukhala munthu.

⁹³ “Ndi chiani izo, ndiye?” inu mungati. Si amulungu atatu. Ndi maudindo atatu a Mulungu yemweyo.

Iye anali Atate, pa chiyambi, yemwe ankapachikika pamwamba—mchipululu mu—mu lawi la Moto, chitsamba choyaka, Utate, Mulungu, monga ndangotsiriza kunena, kudzichepetsa, kubwera pansi. Ilo linali dongosolo lapamwamba kwambiri. Mzimu, a—*agapao*, *Zoe*, m—Moyo wa Mulungu Mwiniwake utapangidwa mwa mawonekedwe a lawi la Moto. Ndipo Mmodzi yemweyo, atatha kukhala mu Utate, anadzakhala Mwana, ndi Mzimu wa . . . unali mu chitsamba choyaka, unali mwa Munthu, Khristu, ndipo Iwo unabweretsa umboni womwewo umene Atate anakachita. Anati, “Ngati ine sindichita ntchito za Atate Anga, musati mundikhulupirire Ine.” Mtengo uliwonse udzachitira umboni chipatso chake chomwe.

⁹⁴ Ndiyeno Iwo utatha kukhala Munthu, onani, Iwo unatsikira pansi kuchokera ku Chauzimu, kukalowa mu chinachake chogwirika chimene chingakhoze kukhudzidwa, thupi. Ndipo kupyolera mu imfa yodzipereka nsembe ndi nsembe yapamwamba ya Mulungu mmodzi uyu, Yesu, Iye anati, “Ine ndi Atate Anga ndife Mmodzi. Atate anga akukhala mwa Ine.” Angakhoze . . . Palibe aliyense yemwe angawerenge izo momveka bwino mwinanso.

Iwo anati, “Nchifukwa chiani Inu simukutisonyeza ife Atate, ndipo izo zitikhutitsa ife.” Yohane 14:8.

⁹⁵ Iye anati, “Ine ndakhala motalika chotere ndi inu, ndipo inu simukundidziwa?” Iye anati, “Pamene inu mwawona Ata- . . . Pamene inu mudiwona Ine, inu mukuwawona Atate Anga.”

Monga dona analumphapo kamodzi; iye anati “Nchifukwa, M’bale Branham,” iye anati, “eya, Atate ndi Mwana ali amodzi, monga momwe inu ndi akazi anu muli amodzi.”

Ine ndinati, “O, ayi, iwo sali.” Ine ndinati, “Kodi inu mukundiwona ine?”

Iye anati, “Inde.”

Ine ndinati, “Inu mukuwawona akazi anga?”

Anati, “Ayi.”

⁹⁶ Ine ndinati, “Ndiye iwo si mtundu womwewo wa mmodzi. Yesu anati, ‘Pamene inu mukundiwona Ine, inu mukuwawona Atate. Atate akukhala mwa Ine.’ Mkazi wanga samakhala mwa ine.” Mukuona?

Iwo ali Mmodzi. Mwa njira iliyonse, iwo ali Mmodzi. Ndipo ife ndi mmodzi kupyolera mchigwirizano, mkazanga ndi ine. Ndife amodzi mu chiyanjano, koma ndife umunthu uwiri. Mkazi wanga akhoza kumachita kuganiza kwa mtundu wina, ndi ine winanso. Ndipo ndife anthu awiri. Koma si chomwecho ndi Mulungu. Iwo, Mulungu ndi Khristu, ndi Munthu yemweyemweyo.

⁹⁷ Ndiye Mzimu Woyera ndi chiani? Mzimu Woyera ndi Mzimu wa Mulungu womwewo ukukhala mwa anthu omwe Iye anawafera, ndipo anaika dzina lawo pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa. Chimene, iwo anali amodzi ndi Iye, pachiyambi. Lemba limanena chomwecho. Kodi Yesu sanawauze iwo kuti iwo anali ndi Iye asanaikidwe maziko a dziko? Malingaliro anu anadetsedwa ndi mdima, ndipo ife tonse tiri, kwa zinthu zimenezo. Koma sindife china chaching'ono chokha chikuchitika mwangozi kuno. Ife ndi ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, pachiyambi cha chilengedwe cha Mulungu, ndipo tinagwetsedwera kungsi kuno kwa umboni, kuti tidzachitire umboni chisomo cha Mulungu chimene chawazidwa mmitima yathu mwa Mzimu Woyera. Ife tiri nawo Mzimu Wamuyaya. Palibe wina, palibe wina, ndipo palibe njira ina, yoleketsera izo. Mpingo wa Mulungu udzakakhalapo uko motsimikiza basi monga izo zingakhoze kukhala zotsimikiza.

⁹⁸ Monga ife tinali kuyankhula, kuti titenge phunziro laling'onolo kachiwiri, basi kwa—kwa miniti, momwe mwana wapathengo sakanakhoza kukalowa ufumu kwa timbadwo fortini, zaka foro handiredi, ndi momwe kuti kusaweruzika kwa makolo kunkachezedwa kwa ana, mpaka ku kam'badwo kachitatu ndi kachinai.

⁹⁹ Ndiponso, chilungamo cha makolo chinkachezedwa. Zomwe inu mukuchita, ngati kukubwera mawa ndipo inu mukadzakhala ndi chidzukululu cha mwanawanu, zochita zanu lero zidzapangitsa chomwe iye ati adzakhale apo.

Pakuti ife timawerenga mu Baibulo pamene kuti Melkizedeki, pamene Iye anakomana naye Abrahamu akubwerera kuchokera kokawapha mafumu, ndipo Abrahamu mbadwa anampatsa Iye chakhumi, chachikhumi cha zonse zomwe iye anali nazo. Ndiyeno iye ananena izo za chachikhumi, kuti, “Levi yekha basi akanakhoza kumalandira chakhumi. Koma,” iye anati, “Levi, yemwe ankalandira zakhumi, anapereka zakhumi pamene iye anali akadali mu chiuno cha Abrahamu.”

¹⁰⁰ O, kodi mungakhoze kumvetsa izo? [M'bale Branham akugogoda pa nsanja kasanu—Mkonzi.] Abrahamu anali wa Levi. . . mdzukululu wa mwana wake. Ndipo apa, Levi, pafupi zaka eyiti kepana teni handiredi mtsogolo, mwinamwake mahandiredi angapo. Ine sindingadziwe basi zingati, zambiri. Ukanayenera kuzilingalira izo, kupyolera mu kam'badwo.

Koma, Abrahamu anabala Isaki; Isaki anabala Yakobo; Yakobo anabala Levi. Ndipo pano, Levi, Yakobo akanati akhale abambo ake; Isaki agogo ake aamuna; ndipo Abrahamu agogoa abambo ake. Ndipo pamene Yakobo anali mu chiuno cha Abrahamu, Baibulo linati, “Iye analipira zakhumi kwa Melkizedeki.”

¹⁰¹ Ndiyeno kam’badwo kakang’ono kano, akuthamanga thamanga, akusuta, kumwa, ndi chirichonse, kodi inu mukuyembekeza kuti kam’badwo kena kadzakhhalapo chotani? Chifukwa chomwe ife tiri ndi tchimo, kupanda khalidwe kwa ana tsopano, chifukwa chomwe ife tiri ndi asungwana aang’ono pa msewu, ndi anyamata aang’ono, ndi chifukwa chakuti amayi awo ndi abambo ankachita zomwe iwo ankachita mu m’badwo wawo unapitawo.

Ndipo chifukwa chomwe ife tikadali ndi alaliki omwe angamaime ndi Choonadi, chifukwa chomwe ife tikadali nao asungwana ena akachitidwe-kachikale, ndi chifukwa iwo anali nao makolo akachitidwe-kachikale kale mmbuyo mwaomo. Ndiko kulondola ndendende. Ife tikadali nawobe alaliki omwe amaima mosanyengerera ndi chipembedzo chirichonse, kapena Mawu, ndi chifukwa kuti ife tinali ndi alaliki akachitidwe-kachikale mmbuyomo, ankaima molondola pa malo omwewo. Inde.

¹⁰² Tsopano ife tiri mu tsiku lino. Ndipo tsopano ife tikufuna kuti tinene, kuti, mkati muno, kubwerera ku...zina za zipembedzo, chifukwa chomwe ife sitiri chipembedzo. Ndipo, chifukwa, ngati ife tikanakhala chipembedzo, ife tikanati tizigwadira kwa izo.

¹⁰³ Ndipo kumbukirani, inu mufufuze Malemba paliponse pomwe mukufuna, ndipo inu simupeza malo amodzi mu Baibulo pamene aliyense anayamba wabatizidwapo mwa kukonkha, mwa kutsanulira, kapena mu dzina la “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” Chotero, ngati siziri mu Lemba, izo zimayenera kuyambira kwinakwake.

¹⁰⁴ Monga ine ndimanena, nditakhala pansu pa mtengo waukulu, ndikuyang’ana pa iwo. Iwo, o, iwo ukhoza kukhala ngati wa—wamphongo, iwo—iwo ukhoza kukhala chachikulu, iwo ukhoza kukhala wamphamvu kwambiri, koma iwo unali ndi chiyambi. Iwo unachita kuyamba. Ndipo chirichonse... Chipembedzo cha nthawi-yachikale ichi chimene ife timaima nacho molimbachi, icho chinachita kuyambira kwinakwake. Icho chinkayenera kukhala nacho chiyambi. Ndipo timalingaliro tomwe ife tiri nato, ito tinayenera kukhala ndi poyambira. Ndipo Malemba abodza omwe ife tikuwagwiritsa ntchito mu zipembedzo zathu, anachita kukhala ndi poyambira. Ndipo ngati ife tikuti, “Ndine wa Methodisti,” inu munachita kukhala ndi poyambira. Ngati inu mukuti, “Ndine wa Baptisti,” inu munachita kuyamba. Inu mukuti, “Ine ndine Mkatolika,” inu munachita kukhala ndi poyambira. Inu mukuti, “Ndine

Mkhristu wobadwa-kachiwiri,” inu munachita kukhala ndi poyambira. Inu munachita kukhala napo apo.

¹⁰⁵ Pitani mmbuyo, kapezeni pamene izo zinayambira. Tiyeni ife tibwerere mmbuyo ku chiyambi cha chithunzi. Ndiye ngati mulibe chipembedzo mu Baibulo, ndiye chipembedzo chinachita kukhala ndi poyambira. Icho chinayamba ndi mpingo wa Katolika. Achiprotestanti ndi mphukira chabe kwa icho.

¹⁰⁶ Ndiye ngati Baibulo limanena kuti iye anali mkazi wa mbiri yoipa, chifukwa cha, chiphunzitso chake, iye anachita ziwerewere zauzimu. Kodi ziwerewere ndi chiani? Kumbukirani, ife tinadutsa mu izo tsopano. Mkazi akamakhala ndi mwamuna wake, iye ali chimodzimodzi monga namwali. Iye sanayambe waipitsidwapo, bola ngati iye akukhala ndi mwamuna mmodzi uyo. Koma kodi kusalungama ndi chiani? Chilungamo, chopotozedwa. Musiyeni iye akhale ndi mwamuna wina, ndipo iye wathetsedwa. Mwaona? Chilungamo, chopotozedwa.

¹⁰⁷ Tsopano, ngati chipembedzo chinali cholakwika... Ngati icho chikanakhala cholondola, Mulungu akananena kuti, “Tsopano ife tati tikhale ndi zipembedzo.” Ndipo ngati... Mpingo wa Katolika unanenedwa, mu Baibulo, monga “hule,” kusalungama, chifukwa iwo unkapereka kwa osonkhana ake zamulungu zake zake, ndipo osati Baibulo. M’bale, mlongo. [M’bale Branham akuwombetsa manja ake kawiri—Mkonzi.] Kodi mpingo wa Katolika sumaseka mu nkhoze yanu pa za Baibulo? Iwo amati iwo samasamala zomwe Baibulo limanena; ndi zomwe mpingo umanena, zomwe chipembedzo chawo chimanena. Chabwino, ndiye, inu mungakhoze bwanji kumawatcha iwo olakwitsa pamene inu mungamagwadire ku ubatizo wa “Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” pamene Baibulo limatsutsa izo? Pakuti Amethodisti amanena chomwecho, Abaptisti amanena chomwecho? Inu mungamavomereze bwanji ku kukonkha ndi kutsanulira, pamene palibe chinthu choterocho mu Baibulo? Mulibe chinthu choterocho kuti aliyense anabatizidwapo mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.” Ndiye nchifukwa chiani inu mumachita izo?

¹⁰⁸ Onani, ndi chifukwa chake ife sitiri chipembedzo. Ife sitimasowa kudyerera kwa iwo. Ife timatenga... Pamene Mzimu uponyera Kuwala pa Lemba, ife timakhala ndi Lemba ndi PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndi inu pamenepo. Palibe zinthu zotero monga izo. Izo sizinalembedwe mu Lemba.

¹⁰⁹ O, inu mukuti, “Nanga bwanji Mateyu 28:19?”

Tsopano, ife tapesa kudutsa mu izo nthawi khumi ndi kawiri. Iyo inali nkhanu yomwe Yesu ananena. “Pitani inu chotero, kaphunzitseni mafuko onse, kumakawabatiza iwo mu Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera.” Kodi izo zinayamba zachitidwapo? Kodi anayamba wakhalapo munthu yemwe anayamba wabatizidwapo mwa njira imeneyo? Palibe mmodzi.

Ndiye payenera kukhala chinachake cholakwika penapake. Zedi, ndi Chikatolika chinazichita izo.

¹¹⁰ Pezani ngati zinayamba zakhalapo mu mbiriyakale, mpaka pa makolo a ante-Nicene, inu azambiriyakale. Muwerenge mabuku a makolo ante-Nicene, ndipo muwone, mpakana kwa mfumu yaku England. Aliyense wa iwo ankabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu mpaka utayamba mpingo wa Katolika. Ndipo mpingo wa Katolika uli nayo mphamvu, iwo amati, kuti azisintha chirichonse chimene iwo akuchifuna. Ndipo iwo anapita nkumakabatiza mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.” Marteni Lutera anaturuka nazo izo. Joni Wesile anazitsatira izo. Ndipo Alexander Campbell anabwera ndi izo. Ndipo John Smith, wa mpingo wa Baptisti, anatsatirabe izo. Ndi izi Chipentekoste chiri nazo izo, pano,

Koma ora labwera!

¹¹¹ Penyani zoyikapo nyali, monga ife tinali nazo usiku watha. Choyikapo nyali choyamba chiri Kuwala. Iko kumapita kukudera, dera, dera, mpaka iko kunadutsa mu zaka fifitini handiredi za mibadwo ya mdima. Ndiye, zinayamba kumayaka aponso. Ndipo basi usanafike m’badwo wa mpingo wotsiriza, iwo unayakanso kachiwiri. Pakati pa mibadwo iwiri ya mpingo, Kuwala kunadza.

Tsatirani Malemba, a mpingo wa Aefeso, mpingo wa Atesalonika, mpaka mmusi ku m’badwo wa mdima. Uliwone wa iwo, Iye anati, “Inu muli nazo mphamvu pang’ono, koma inu simunalikane Dzina Langa.” Ndipo mpingo wotsatira, “Inu mwachita chinthu chachikulu, koma inu simunalikane Dzina Langa.” Tsatirani makolo a ante-Nicene kutsika kudutsa nazo. “Inu simunalikane Dzina Langa.” Ndiye, zaka fifitini handiredi za mibadwo yamdima.

Ndiye mpingo wa Chilutera unatuluka. Iye anati, “Inu mulibe Dzina Langa, koma inu muli nalo dzina.” Osatinso Yesu; koma Lutera, ndi Katolika, ndi Baptisti, ndi Presbateria. [M’bale Branham akuwombetsa manja ake kawiri—Mkonzi.] “Inu muli nalo dzina kuti ndinu amoyo. ‘Ndife mpingo wamoyo. Ife tikulimbikira. Ife tikupita patsogolo.’ Koma inu muli akufa!” Malemba amanena chomwecho.

¹¹² “Pakuti palibe dzina lina linaperekedwa pansu pa Kumwamba pakati pa anthu, limene anthu angapululumutsidwe nalo.” Osati... Baptisti siikupulumutsani inu. Presbateria siikupulumutsani inu. Katolika siikupulumutsani inu. Yesu amakupulumutsani inu.

¹¹³ Zonse mu timabuku tating’ono, nthano zopangidwa ndi anthu, iwo amazilemba izo, “Ndi chimene ife timachikhulupirira.” Ndipo ndi chifukwa ife timakhala kutali kwa izo. Ife tiribe bukhu lowerenga koma Baibulo. Tiribe kutsogolera, tiribe bishopu, koma Mzimu. Ndiko kulondola.

Ndiyeno ngati pali mzimu wolakwika ukubweramo, uyesa kupotozera chinachake mmenemo, Mawu adzachotsa kupotokako. “Ndi kulakwitsa. Khalani kutali nazo.” Mwaona? Apa panadza Mzimu motsatira, ukuti, “Uko nkulakwitsa.” Ukuchitira umboni, pakuti mzimu wathu umachitirana umboni ndi Mzimu Wake.

Apa padza wina motsatira, akuti, “O, ife tiyenera. O, ine ndikuganiza ndi zabwino iwo kuti azichita *izi, izo, zinazo.*”

¹¹⁴ Koma Mzimu unati, “Pali chinachake cholakwika ndi izo.” Umapita mmbuyo pansi mu Baibulo ndi kuzibweretsa izo mmusi momwe, momwe ife tikuchitira. “Ndipo izo nzolakwika. Khalani kutali nazo.”

Ndicho chifukwa Baibulo linati, “Pano ziri kwa iye yemwe ali nayo nzeru. Pano ziri kwa iye yemwe ali nacho chidziwitso. Pano ziri kwa iye yemwe ali ndi *izi.*” Mpingo uko, ukukhala mu dongosolo. Kodi inu simukuona dongosolo lalikulu la Mulungu?

¹¹⁵ Tsopano penyani. M’badwo wa Mpingo wa Filadefia unali m’badwo wa mpingo wa Methodisti, m’badwo wa mpingo wa chikondi cha paubale, kukonzanso. Kumene, pamene Chikalvani chapamwamba chinatulukira mu mpingo wa Anglikani ku England, kumene iwo analibe nkomwe chitsitsimutso aponso, anapita mpaka ku mbewu za zoyambirira, Mulungu anamuutsa John Wesile ngati wa mwamalamulo, kuti atenge chiphunzitso cha chi Arminiani. Ndipo pamene iye anatero, iye anachigogoda chinthu chimenecho pa mutu, ndipo icho chinkayeneredwa kutero. Koma nchiani chimene iye anachita? Apa panadza Amethodisti motsatira, ndipo anathamanga patali basi mjira *imeneyo* monga iye (Chikalvini) anachitira mwa njira *imeneyi*. Tsopano, pakati pakepo, pakadali Amethodisti, pakadali Abaptisti.

¹¹⁶ Ndikukhumba ife tikadafika mpaka kuno tsopano mu Malemba, Kutenga Chivumbulutso 3, ndipo inu mumva izo. Tsopano basi tisanati. . . M’badwo wa mpingo wotsiriza, umene unali wa Chipentekoste, ndi wofunda, M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya, umene uli wokanidwa.

Koma kumbukirani, monga Yesu anawonekera mu mtanda, ataima mu zoikapo nyali zagolide zisanu ndi ziwiri, wamdima kwambiri unali umene unali kutali ndi Iye, dzanja Lake lamanja ndi dzanja Lake lamanzere. “Ndipo Iye anali woti ukamamuyang’ana ngati Alfa ndi Omega.” Osati pakati pakepo. “A—Alfa ndi Omega,” pamene Iye anali atatambasula dzanja Lake. “Ndipo Iye anali mwala wa yaspi ndi wa sardio,” umene unali Benjamini ndi Rubeni, “woyamba ndi wotsiriza.” Apo Iye anali ndi manja Ake atawaongola. Apo Iye anaima.

¹¹⁷ Koma kumbukirani, pa kutuluka kwa izi, musati muzisokoneze izo. Pakuti, pamene iwo analandira maina awa apa, a zipembedzo izi, iwo akanafa mu zinthu izo zomwe,

mpaka pansi. Koma Iye anati, “Basi pakati pa Amethodisti ndi Achipentekoste, ukuchokamo, “Ine ndaika khomo lotseguka patsogolo panu.” Ndi inu apo, Dzina likubwezeretsedwa kachiwiri. “Ine ndaika khomo lotseguka. Pakuti Ine ndine Njira, Choonadi, ndi Moyo. Palibe munthu amadza kwa Atate kupatula kudzera mwa Ine.” Nchiani icho? Khomo lotseguka ilo.

¹¹⁸ “Khwalala!” Khwalala, ngati inu mungazindikire, si s-t-r-a-i-g-h-t. Ndi s-t-r-a-i-t. “Khwalala ndilo njira.” Khwalala, ndi madzi.

Motani? “Kubwerera ku Dzina la Yesu, limene inu munali nalo. Inu mulibe. . . Muli nawo moyo pang’ono; inu simunalikane Dzina Langa.” Ndiye, ndiye, *umu* iwo analitaya ilo, anapita mu chipembedzo cha Chikatolika; anatuluka mu chipembedzo cha Chilutera, anatuluka mu chipembedzo cha Wesile, ndiye iwo akupita mpaka mu Chipentekoste apo.

Koma, isanafike kumene nthawi yotsiriza, Mbewu yatsala pang’ono kupita kuchokera pa dziko lapansi. Iyo yayenda kutulukamo, Mbewu ya olungama. Mbewu ya serpenti ikumangowunjikana mofulumira fulumira fulumira, kukonzekera m’badwo wa atomiki uno, kuti iwonongedwe. “Koma basi isanafike nthawi imeneyo, Ine ndidzaika njira yothawira. Ine ndidzaika patsogolo panu khomo lotseguka. Khwalala ndilo chipata ndipo njirayo ndi yopapatiza, ndipo adzakhalapo apang’ono okha a iwo ati adzaipeze iyo. Koma yotambalala ndi njira yolondolera ku chiwonongeko, ndipo ambiri ndiwo ati adzapite mu imeneyo.” Ndi inu apo. Basi zisanati izi, Kuwala kwakukulu uku kumayenera kuti kutumphukirepo.

¹¹⁹ Ndine wokondwa kwambiri. Ine sindikudziwa basi momwe ndingafotokozere izo, ndine wokondwa kwambiri. Ndi izi pano, nthawi yoti nditseke, ndipo ine sindinalikhudze konse phunziro langa.

¹²⁰ Ine ndikufuna kuti ndiyankule pa: *Ubatizo Wa Mzimu Woyera*. Ine ndikuti ndikhudze izo, mulimonse, kwa maminiti khumi, khumi ndi asanu. Tsopano, ine sindikusungani inu maora atatu monga ine ndinachitira usiku wathawu; ine ndiyesera ndisatero.

¹²¹ Tsopano, ngati iwo ali ndi ubatizo wabodza wa madzi, zipembedzo ndi zolakwitsa. Ndipo yense yemwe amaikira kumbuyo zipembedzo zinazake mwamtheradi akuthandizira chinthu cholakwika. Iwo akuthandizira zomwe Mulungu akutsutsana nazo. Ananena chomwecho mu mibadwo ya mpingo iyi. Ananena chomwecho mu Lemba, ndipo anawatcha iwo aziwerewere, chifukwa, “Iwo amaphunzitsa ngati Chiphunzitsa malamulo a anthu.” Tsopano, ife. . .

¹²² Ine ndinapita ku malo osati kale litali, kwa munthu wina anabwera muno, amalemba nkhani ya machiritso Auzimu.

Ndipo iye anati, “Chinthu chokha chokhudza inu, M’bale Branham,” anati, “anthu akugwira potsutsa inu chifukwa inu mumapita kwa Achipentekoste.”

Ine ndinati, “Chabwino, ine ndizibwera ku chanu,” ine ndinati, “ngati inu muti mudzandithandizire ine mu mzinda wanu.”

Iye anati, “Chabwino,” anati, “Ine—ine ndinazitenga kale izo.” Anati, “Ine ndinazitengera izo kwa a bishopu a mpingo *wakuti* uwu, mpingo wa Methodisti.” Palibe chifukwa chobwezera nkhonya iliyonse pa izo. Anati, “Ine ndinazitenga izo, ndipo iwo anati, ‘Tsopano, inu mukuona, ife, monga mpingo wa Methodisti, sitimakhulupirira mu zozizwitsa izi.’”

¹²³ Tsopano kodi inu muchita chiani? Tsopano kodi inu mumvetsera kwa mpingo wa Methodisti, kapena chipembedzo? Ngati inu mutero, ndinu wachipembedzo mwachiwerewere. Inu mukuganiza mpingo wa Baptisti ukanati uhandizire msonkhano wokopa woterowo? [Osonkhana ati, “Ayi.”—Mkonzi.] Bwanji? Chifukwa iwo ndi Abaptisti. Baibulo linati iwo ndi achiwerewere. Iye anabala ana ake aakazi, ndipo iwo anali “timahule.” Chifukwa? Akupereka chiphunzitso cha mtundu womwewo, chiphunzitso chopangidwa ndi munthu, mmalo mwa Chiphunzitso cha Mulungu. Ndi chifukwa ife si achipembedzo nawo Abaptisti. Ndi chifukwa ife si achipembedzo nawo Amethodisti.

¹²⁴ Tsopano, chifukwa chiani ife si achipembedzo ndi Achipentekoste? Ndi inu apa. Ziri chimodzimodzi. Achipentekoste akanati akhale pamene. . . Ngati—ngati mpingo wa Chilutera ukanati ukhale pamene iwo unayambira, iwo ukanakhala uli wa Chipentekoste. Koma iwo anapanga chipembedzo, koteru Mulungu anautsa wa chipentekoste wina, wotchedwa Wesile. Ndipo koteru pamene Wesile anapanga chipembedzo, Iye anautsa wina, wotchedwa Baptisti. Pamene iwo anapanga chipembedzo, ndiye Iye anautsa wina, wotchedwa achi Campbell. Pamene iwo anapanga chipembedzo, Iye anautsa wina, wotchedwa Pentekoste. Pamene iwo anapanga chipembedzo, Iye akusunthabe napitirira. Ingopenyani ndipo muwona.

¹²⁵ Iyo si programu Yaumulungu ya Mulungu. Izo siziri mu programu ya Mulungu, kuti akhale ndi zipembedzo zimenezo. Koteru, inu mukuona, ndi chifukwa chomwe ife sitiri chipembedzo.

¹²⁶ Kumbukirani ichi. Ine ndinanena, poyamba, tsopano, ngati ine ndikupwetekani inu, ine sindikutanthauza kutero. Izi ndi za mpingowu. Ngati inu mwakhala nawo, ife tikukonda kukhala nanu muno, koma izi ndi zomwe ife timaima nazo, ndi chifukwa chomwe ife sitiri achipembedzo.

¹²⁷ Tsopano, chipembedzo, pa kuyamba pomwe, ndi chabodza, ndi aphunzitsi abodza. Ine ndinati izi zipweteka, ndipo ine ndikufuna kuti izi zipweteke. Iwo mwamtheradi ndi aphunzitsi abodza. Munthu aliyense yemwe amazidziwa zinthu izo, ndipo nkumaima ndi kumawanyengerera, Abaptisti, Amethodisti, Achilutera, kapena Achipentekoste, akudziwa kuti Baibulo limaphunzitsa zosiyana, iye ndi mneneri wabodza. Musamamatire pozungulira izo. Ndizo ndendende. Ndi chifukwa ine sindinawajowine a Assemblies. Ndi chifukwa ine sindinawajowine Aumodzi. Ndi chifukwa ine sindinajowine Abaptisti, Amethodisti, kapena Chipresbateria, chifukwa iwo ndi abodza. Ine sindikutanthauza kuti anthu awo ndi abodza. Ine ndikutanthauza zamulungu zawo ndi zabodza, chifukwa izo sizimafanana ndi Mawu a Mulungu.

Paulo anati, “Ngati . . .” Iye anapita mpaka uku . . . Ndiroleni ine ndikusonyezeni inu zomwe Paulo ananena, tisanausiye ubatizo wa madzi uwu.

¹²⁸ Pamene Yesu analamula, mu Mateyu 28:19; Petro, masiku khumi mtsogolomo, anati, “Lapani aliyense wa inu ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha machimo anu, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.”

Nthawi yotsatira yomwe ubatizo unatchulidwa, pamene Filipo mlaliki anapita kwina ndipo anakalalikira kwa Asamaria. Ndipo iye anabatiza aliyense wa iwo mu Dzina la Yesu Khristu. Paulo . . . Petro anabwera uko, kapena Petro ndi Yohane, kani, ndipo anadzaika manja pa iwo; iwo analandira Mzimu Woyera.

Ndiye iwo anapita uko. Petro anapita molunjika ndiye ku nyumba ya Kornelio. Ndipo pamene Kornelio . . . “Pamene Petro anali chiyankhulire Mawu awa, Mzimu Woyera unagwera pa iwo.” Petro anati, “Ife sitingakhoze kuwaletsa madzi, powona kuti awa alandira Mzimu Woyera monga ife tinachitira pa chiyambi.” Ndipo iye anawalamulira iwo kuti abatizidwe mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu.

¹²⁹ Tsopano, Paulo anadutsa ku maiko aku mtunda kwa Efeso; iye anawapeza Abaptisti ena. Ndipo iwo anali—iwo anali naye mtumwi uko, mtumwi wa Baibulo, ndipo dzina lake anali Apollo. Iye anali wazamalamulo, wotembenezidwa, ndipo iye anali akutsimikizira kwa anthu kuti Yesu anali Khristu, ndi Baibulo. Iye anati, “M—Mesiya akuyenera kudzachita zinthu zinazake. Munthu uyu anali Mesiya.”

¹³⁰ Ndipo iwo anali ndi gulu lalikulu la anthu uko, ndipo iwo anali akusangalala, ndi kumafuula, ndi kumakhala nayo nthawi yaikulu ya izo. Akwila ndi Prisila anali atapita uko ndipo anakalumikizana nawo, ali ndi chiyanjano nawo. Iwo analibe chipembedzo. Iwo anangokhala ndi chiyanjano. Ndipo koteru iwo anamuwona munthu uyu kuti anali munthu wamkulu, o,

iyе ndi wanzeru, woweruza mlandu, ndipo iyе anali—iyе anali bambo wanzeru. Chotero iyе. . . Iwo anati, “Tsopano, inu, inu ndinu abwino kwambiri pa zomwe inu mukuzidziwa, koma ife tiri naye m’bale wamng’ono wotchedwa Paulo. Pamene iyе abwera, iyе anali nazo zomuchitikira zina, iyе akudziwa zomwe iyе akuzikamba. Iyе adzakuphunzitsani inu njira ya Ambuye momveka kwambiri, ngati inu mudzangokhala ndi kumamvetsera kwa iyе. Tsopano, musati muyesere kukankhira chinachake pa iyе, chifukwa iyе sadzaima duu kwa izo. Mwaona? Koma inu basi—inu musingodzapitirira, kumamvetsera kwa iyе.”

¹³¹ Ndipo Paulo anabwera modutsa. Iyе anamvetsera kwa iwo, anayang’ana kamodzi pa iwo.

Iyе anati, “Ndi zabwino kwambiri, koma kodi inu munalandira Mzimu Woyera, inu Abaptisti, kuchokera pamene inu munakhulupirira?”

“O,” iwo anati, “kodi ife tiribe Iwo?”

“Sindikuganiza chomwecho.” Mwaona?

“Chabwino, motani?”

“Chabwino, nanga inu munabatizidwa chotani?”

“O, ife tinabatizidwa kale. Ife tinabatizidwa kale.”

¹³² “Chabwino, ndani anakubatzani inu? Ndipo kodi inu munabatizidwa chotani?”

Baibulo limati, “kwa chiani.” Chigriki, kapena mwapachiyambi, limati, “motani.” Ndipo ili likuti, “*kwa chiani.*” Anati, “Kodi inu munabatizidwa kwa chiani?” Mwa kuyankhula kwina, “Kodi inu munabatizidwa chotani?”

¹³³ “Ife tinabatizidwira kwa Yohane M’batizi, munthu yemweyo amene anamubatiza Yesu Khristu, dzenje lomwelo la madzi.”

Ndiwo ubatizo wabwino kwambiri, kodi inu simukuganiza chomwecho? Zikuwoneka ngati izo zikanagwira bwino bwino, si choncho? Zikuwoneka ngati zikanakhala ziri bwino, ngati munthu yemwe analowa mmadzi ndi Ambuye wathu Yesu Khristu namubatiza Yesu. Ndipo Mulungu anazivomereza izo, mpaka Iyе anatsika pansi mwa mawonekedwe a Mzimu Woyera ndipo anadalawa mwa Iyе. Ndipo Iyе anati, “Uyu ndiye Mwana Wanga wokonedwa mwa yemwe ine ndimakondwera kukhalamo,” utangochitika ubatizo umenewo. Zikuwoneka kwa ine ngati ubatizo umenewo ukanakhala wabwino.

¹³⁴ Ndipo Paulo anati, “Iwo sugwiranso ntchito tsopano. Siwugwira ntchito panonso.”

“Chifukwa chiani kuti sugwira ntchito panonso?” Mwaona?

“Inu muyenera kuti mubatizidwenso kachiwiri.”

“Inu mukutanthauza kuti ife, omwe tinabatizidwa ndi Yohane, yemwe anamubatiza Yesu, tiyenera tibatizidwenso?”

“Ndiko kulondola.”

Anati, “Ife tiyenera tibatizidwe chotani?”

135 Anati, “Mu Dzina la Yesu Khristu.”

Ndipo Paulo anawatengera iwo uko apo ndipo anawabatiza iwo onse, kachiwiri. Machitidwe 19:5. “Ndipo pamene iwo anamva izi, iwo anabatizidwa kachiwiri, tsopano, mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo Paulo anaika manja ake pa iwo, ndipo iwo analandira Mzimu Woyera.”

136 Ngati Paulo ankawakakamiza amuna ndi akazi kuti abatizidwenso kachiwiri, mu Dzina la Yesu Khristu; ngati ine ndalalikira Uthenga wina uliwonse, ndiye mzimu wanga si wolondola monga wa Paulo unaliri. “Mulole iye azindikire kuti zomwe ine ndikulemba ndi malamulo a Ambuye.”

137 Ndipo tsopano mu Agalatia 1:8, Paulo anati, “Ngati mngelo wochokera Kumwamba abwera, mngelo wowala monyezimira.” Kodi iye akunena za chiani? Vumbulutso. Lidalitsike Dzina la Ambuye! Ziribe kanthu kuti vumbulutso lako ndi labwino chotani. Inu mukukumbukira poyamba pa msonkhano wathu mmawa uno, Urimu Tumimu? Ngati chinachake chibwera ndi kudzaulula izo mwangwiro; iye ndi wabodza, iye ndi mngelo wabodza, ndipo munthu yemwe angatenge uthenga wake ndi mneneri wabodza. Ilipo njira imodzi yokha yoti ubatizidwire, ndiyo mu Dzina la Yesu Khristu. Ngati inu simunabatizidwe mwanjira imeneyo, alipo malo obatzira akuyembekeza. Ndiko kulondola.

138 Mwabodza! Ndipezereni ine malo amodzi pamene aliyense anayamba wabatizidwapo mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.” Izo siziri mu Zolemba zopatulika. Ndi chiani icho? Ndi mbalume imene inayambitsidwa ndi mpingo wa Katolika. Ife tikhoza kuthandizira izi. Ife tiri nazo ziphunzitsa za makolo a Ante Nicene. Ife tiri nayo mbiriyakale ya izo. Ife tiri nalo la *Two Babylons* la Hislop. Ife tiri nazo zolemba za Josephus. Ife tiri nazo mbirizakale zonse zamakedzana. Ndipo Josephus analemba mu nthawi ya Ambuye Yesu. *Two Babylons* la Hislop, analemba pambuyo pa ilo. *Ante Nicene Fathers* analemba pambuyo pa ilo, usanapangidwe mpingo wa Katolika. Ndiyeno mpingo wa Katolika unabweramo, ndipo unadzakankhira izo zonse panja ndipo unadzalandapo, iwoeni, ndipo Roma wachikunja anapangidwa kukhala Roma wa upapa. Ndipo apo iwo anabweretsa ubatizo wabodza wa madzi uwo, wa kukonkha; ndipo kuchoka pa Dzina la Ambuye Yesu, kukhala “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.” Ndipo Yesu anati, pansi pa kudzoza kumene Iye anakupereka kwa Yohane pa Patmo, “Inu muli nalo dzina loti muli moyo, koma ndinu akufa.” “Atate, Mwana, Mzimu Woyera” ndi dzina lakufa.

¹³⁹ Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chondichitikira changa chaching’ono; Switzerland, Germany, ndi malo kumene ine ndakhala ndiri.

Kodi ambwebwe amagwira ntchito motani? Kodi mizimu yoipa imayenda motani? Ine ndikufuna kuti inu mundikhulupirire ine, monga m’busa wanu, chifukwa ndinu omwe ine ndikuyankhula nanu. Adierekezi amayenda mu dzina la “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” Iwo amadula nthenga, ndi china chirichonse, ndi kuponyerana matsenga pa wina ndi mzake, kupyolera mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” amawatcha iwo maina atatu apamwamba. Mayi wake wa zimenezo ndi mipingo ya Katolika. Iwo amapita kwa zoimikidwa izi ndi kugwada apo, ndi kumadula nthenga ndi sisesi, ndi kuzitembenusa izo chammbuyo, ndi kuponyera matsenga pa oyandikana nawo, ndi zina zotero, kumene iwo amakawotchedwa mpaka imfa, ndi china chirichonse, chifukwa cha izo.

¹⁴⁰ Mu Switzerland, ine ndinaima ndi manja anga ali pa mtengo, monga *choncho*, kumene amuna owona mtima ndi akazi anafa, pamene iwo ankadula malirime awo, ndi kuwotcha maso awo kuwachotsamo, ndi chirichonse, ndi zitsulo zamoto, mpingo wachiwerewere wa Katolika uwo. Osati iwo okha, koma mipingo yanu yoyambirira ya Angilikani, nayonso. Ndi mipingo yanu ya Chiprotestanti inachita chinthu chomwecho. Ndipo iwo anaponyera matsenga awo, mu “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.”

¹⁴¹ M’bale wanu ndi m’busa, ine ndakhala nawo—mwayi woyamikira, mwa chisomo cha Mulungu, kuti nditetezedwe kwa zinthu izi, koma kuti ndizidziwa moyambirira zomwe ine ndinali kuzinena. Kumene mkazi, anali kubwera ku mpingo uno, nkumanditsutsa ine ndi kuti, “Iye akuwapusitsa ndi zamizimu.” Mulungu Kumwamba akudziwa chomwe zonse izo ziri. Ine sindingakhoze kutenga za munthu wina . . . ine sindinati . . .

¹⁴² Pamene iwo anandiuzwa ine kuti Pigalle, mu Paris, anali malo a mbiri yoyipa chotero, ine ndikanadziwa bwanji? Ine ndisanapiteko uko nkomwe. Koma ine ndinapita uko kuti ndikapeze ngati izo zinali zolondola kapena ayi. Ine ndinawatenga atumiki awiri kapena atatu ena ndipo tinapita uko kwa akazi awa ndi zinthu zomwe amazivula pa misewu iyo ndi zinazo. Ndi zoon.

¹⁴³ Ine ndikanadziwa bwanji kuti Roma ali pa mapiri seveni? Ine ndikanadziwa bwanji kuti papa anali ndi VICARIVS FILII DEI? Ndikanati ndizitenga mawu a winawake pa izo. Ine ndikanadziwa bwanji kuti nduwira ya patatu inali pa papa; ulamuliro wa wolowammalo wa Kumwamba ndi dziko lapansi ndi hade? Ine ndikanadziwa bwanji izo mpaka ine nditapita ndi kukaziwona izo?

¹⁴⁴ Kodi ine ndikanadziwa bwanji kuti kuli Mulungu wamoyo? Osati pansi pa zamulungu za winawake, lingaliro lina laluntha la nyengo yotengeka yomwe inadutsa kupyola mu m'badwo ukudutsawu, momwe achikunja angatiuzire ife. Koma tsiku lina, kutsidya uko, ine ndinampeza Iye ndi ngakhale kuyankhula kwa Iye, maso ndi maso. Izo zimapangitsa zinthu kusiyana. Kulondola ndendende.

¹⁴⁵ Zamizimu zimagwira ntchito kupyolera mu "Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera." Ine ndinaima mu msonkhano kumene mfiti izo zinali kugwira ntchito. Musati inu muganize kuti izo sizingakutsutseni inu. Izo zinaima pamenepo. Izo zinaponyera tebulo mmwamba, ndipo iyo inkayandama ikuzungulira; ndipo gitala ikuimbidwa. Nditaima pamenepo, ndipo iwo ankafuna kuti anditulutsemo ine. Ine ndinati, "Inu mukulakwitsa." Ndipo Mzimu unayankhula moyankha kwa iwo, mzimu unavomereza kuti ndi Mulungu, unati uyo ndi Mulungu. Ine ndinati, "Ndi zolakwika. Ndi mdierekezi."

Iwo anati, "Munthu uyu ndi wosakhulupirira."

¹⁴⁶ Ine ndinati, "Ndine wosakhulupirira kwa zinthu izi, chifukwa izo si za Ambuye wanga. Uwu ndi ufiti. Izi ndi za Mdierekezi." Ine ndinati, "Tsopano, pano ine ndiyesera Dzina lamphamvu ilo limene ine ndinabatizidwira nalo." Ine ndinati, "Mu dzina la 'Mmwamba mokwera,' ndiuzeni ine zoono." Sizimandiyankha konse ine. Ine ndinati, "Mu dzina la 'Mpingo woyera,' ndiuzeni ine zoono." Iye sanandiyankhe ine. Ine ndinati, "Mu dzina la 'Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,' ndiuzeni ine zoono." Ndipo iye sanandiyankhe ine. Koma, ine ndinati, "Mu Dzina la 'Yesu Khristu,' ndiuzeni ine zoono."

¹⁴⁷ Iye anati, "Inde. Ndi zolakwika." Mulungu akudziwa kuti izo ndi zoono. Inde, bwana. O!

Chikhulupiro mwa Atate, chikhulupiro
mwa Mwana,
Chikhulupiro mwa Mzimu Woyera, atatuwa
ndi Mmodzi;
Adierekezi adzanjenjemera, ochimwa nauka;
Chikhulupiro mwa Ambuye Yesu
chimanjenjemeretsa chirichonse.

Inde, bwana. Khalani pafupi ndi Dzina limenelo.

¹⁴⁸ "Inu muli nalo dzina loti ndinu amoyo, koma ndinu akufa." Ndi umenewo mpingo wanu. Ndi izo apo.

¹⁴⁹ Mvetserani. Alipo mkazi mmodzi wakhala . . . Akazi abwino, owoneka-bwino, okongola omwe akhala mu mpingo muno mmawa uno. Asungwana, akazi a usinkhu-wapakati, akazi achikulire, iwo onse ndi abwino. Iwo ndi mkazi wa winawake, mwana wamkazi wa winawake, wokoma mtima wa winawake, ena otero. Iwo ali, aliyense. Pali Akazi a William Branham amodzi ali muno. Ndinu, aliyense, akazi. Koma pali Akazi a

Branham amodzi. Iyeyo ndi yemwe amapita kunyumba ndi ine. Iye ndi yemwe ali wokoma mtima wanga. Iye ndi yemwe akulera ana anga.

¹⁵⁰ Iipo mipingo yambiri yabwino mu dziko lero. Koma pali Mkazi wa a Yesu mmodzi yemwe akubala enieni, zoono, obadwa kachiwiri olengedwa ndi Mulungu. Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza, sichoncho inu? Dzina lake si Methodististi. Dzina lake si Baptististi. Dzina lake ndi Yesu, Akazi a Yesu. Zedi, Iye ali. Iye akubala anthu, osati mamembala a mpingo wa Methodististi. Iye sakubala mpingo wa Baptististi, kapena wa Presbateria, kapena Katolika. Iye akuwabala iwo, obadwa, ndi ozikika ndi okhazikika mwa Khristu Yesu. Ndi Uyo apo. Ndi Ameneyo. Ndine wokondwa kuti ndiri ndi Iye. Iyeyo ndi Mpingo wachinsinsi. Iye alibe chipembedzo chirichonse. Iye satenga lirilonse la maina aakulu okopa awa ndi zinyumba zazikulu. Iye amasonkhana paliponse pamene ziwalo za Thupi zisonkhana pamodzi. Iwo amapembedza mu Mzimu ndi mu Choonadi. Iwo anakonzedweratu asanaikidwe maziko a dziko.

Lemba limodzi lina, ndipo ine ndikukulonjezani inu ine nditseka. Ndipo ine ndizisiyira zina zonse za izo mawa usiku. Leo, iwe ukhoza kuzigwira izo usikuuno, ndiye.

¹⁵¹ Tiyeni tipite ku Aefeso, miniti yokha. Tingowerenga Lemba limodzi ili, ndiye ine ndizisiyira izo kwa inu. Iye tipeza zomwe Baibulo likunena tsopano pa izi. Ine ndikuti ndimutenge mphunzitsi wamkulu uyu, Paulo, amene ali... Sipanayambe pakhala wina wonga iye. Iye anali mtumwi kwa Mpingo wa Amitundu. Chabwino. Pezani Aefeso 1.

¹⁵² Tsopano ife tikuti titseke, mu miniti yokha. Mvetserani kwa izi, mzanga wokondedwa. Mvetserani kwa Paulo akulalikira kwa Mpingo wa mtundu womwewo umene ine ndirimo, mmawa uno.

Paulo, mtumwi wa Yesu Khristu mwa chifuniro cha... (mpingo wa Presbateria? Mpingo wanji?)... chifuniro cha Mulungu, kwa oyerera (oyerawo) omwe ali ku Efeso,...

Tsopano, kumbukirani, iwo amwazikana konsekonse pa dziko. Koma, ili ndi gulu laku Efeso, limene iye akuyankhula nalo. Tsopano, iye sakuyankhula kwa dziko. Iye sakuyankhula kwa mamembala a mpingo wamba. Iye akulondolera izi kwa oyerawo. Tiyeni tiwone.

... ndi kwa okhulupirika mwa Khristu Yesu:

Ife timalowa bwanji mwa Khristu Yesu? “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa,” kumakhala mokhulupirika. Iwe umadziwa bwanji kuti uli nawo Mzimu Woyera? Ife tifika ku izo mwinamwake usikuuno. Mwaona? Chabwino.

... mwa Khristu Yesu:

Chisomo chikhale kwa inu, ndi mtendere, wochokera kwa Mulungu Atate athu, ndi . . . Ambuye Yesu Khristu.

Adalitsidwe Mulungu ndi Atate wa Ambuye wathu Yesu Khristu, yemwe watidalitsa ife ndi madalitso onse auzimu mmalo ammwambamwamba . . .

¹⁵³ Inu mukudziwa, izo sizimatengera kufuula kochuluka. Izo sizimatengera kukuwa kochuluka. Izo ndi zabwino; palibe chotsutsa izo. Ndi zabwino. Izo sizimatengera zimenezo. Izo zimatengera—mtima wodzipereka, kumakhala mu malo Ammwambamwamba, kumadyerera pa zinthu za Mzimu. Ndipo kodi Mzimu umadyerera pa chiani, kutengeka? Osati zonse palimodzi. Iwo umabweretsa kutengeka. Mwaona? Koma iwe ukhoza . . .

¹⁵⁴ Kumbukirani. Inu mukukumbukira masomphenya okhudza mvula ndi tirigu, namsongole? Kumbukirani. Pamene anasowa mvula, panali chisoso chaching’ono, icho chinali ndi mutu wake utazyolika pansi; tirigu anali ndi mutu wake utazyolika pansi. Pamene mvula inabwera, onse a iwo amalumphamwamba ndi kufuula. Mvula yomweyo. “Koma ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo.” Penyani.

Chisomo chikhale kwa inu, . . . ku—kuchokera kwa Mulungu atate athu, . . .

Tsopano penyani. “Malingana . . .” Ndime yachinai tsopano.

Malingana monga iye anatisankha ife mwa iye . . .

Pa chitsitsimutso chathachi? [Osonkhana, “Ayi.”—Mkonzi.] Anha? [“Ayi.”] Pamene ife tikhala membala wa Baptisti kapena Mate- . . .? Ayi. “Anatisankha,” iwo asanakhale ndi msonkhano. Eya.

. . . asanaikidwe maziko a dziko, . . .

Iye anatisankha ife apo pomwe. Osati, ife sitinamusankhe Iye. Iye anatisankha ife. Mwaona? Iye anatisankha ife apo asanaikidwe maziko a dziko.

. . . kuti ife tikhale tiri oyera . . .

¹⁵⁵ Kodi ife tinali oyera chotani? Osati kupyolera mu zomwe ife tinachita, koma zomwe Iye anatichitira ife, chifukwa ife sitingakhoze kukhala. Inu mungakhoze bwanji kuipanga nkumba kukhala mwanawankhosa? M’bale Roy, inu munkaweta nkumba ndi nkhosa, zonse. Inu simungakhoze—inu simungakhoze kuzisakaniza izo. Nkhumba basi. . . iye amapita uko ndi kukadya mtundu wa zakudya ziri zonse zomwe iye angakhoze. Iye amafika pa mulu wa ndowe ndi kuzidya zodzaza mimba. Chabwino, inu simumamverera kuipidwa ndi izo. Inu mumaganiza kuti nkumbayo ili bwino basi. Iyo ndi nkumba yabwino basi. Ndizo zonse. Koma inu simumaiwona nkhosa cha kumeneko. Iye sakanakhoza kumuitanira iye ku nkhomaliro; iye sakanakhoza kubwerako.

Ayi. Chavuta ndi chiani? Chifukwa, iye ndi nkumba. Inu mukapita kukamuuzza iye kuti akulakwitsa. “Mulungu adalitsike, ine ndine nkumba. Iwe zikhala pa malo akowo. Iwe zipita uko, ukakhale woyera-wodzigudubuza ngati iwe ukufuna kutero.” Ndi inu apo.

“Ngati inu mulikonda dziko kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri mwa inu nkomwe,” anatero Mawu.

¹⁵⁶ Tsopano, osati chifukwa ine ndinasiya kudya manyowa, zandipanga ine kukhala wosiyana ndi nkumba, mwaona, zandipanga ine kusakhala nkumba panonso. Izo sindizo ayi. Koma pamene chikhalidwe changa chinasintha. “O, iwo aika mpanda pondizungulira, ine ndikuganiza. Iwo anditchingira. Ine sindikuyenera kumachita *izi*”? O, ayi. Iwe sumadzitchingira chirichosne kwa ichi. Iwe umangobadwa mwatsopano. Ndizo zonse. Iwe umangosinthidwa. Ndiko kulondola.

¹⁵⁷ Koma ngati inu mungakhoze kuutenga mzimu kuchokera mwa—mwa nkhusa iyo ndi kuwuika iwo mwa nkumba; mwanawankhosa uyo angamachite zinthu zomwezo. Nkumba ingamachite zinthu zomwezo mzimu wa mwanawankhosa umene uli mwa iye ungamachite, ndipo mwanawankhosa uyo angatembenuke apo pomwe ndi kumachita zinthu zomwezo zimene nkumba imachita.

Tsopano inu mukuona, inu nkumba, pomwe muli? Mwaona? Ndiko kulondola ndendende. Ndi kulondola. Mwaona? Inu mumapitabe kunja ndi kumakonda zinthu za mdziko, kumavala zazifupi ndi kumachita zinthu zonse izi. Zipitirirani, zikusonyeza chomwe inu muli.

¹⁵⁸ “Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo. Kodi munthu amathyola nkhyu kuchokera pa minga?” Mukuona? Ayi, ayi. Inu mumathyola nkhyu kuchokera mu mitengo ya mkuyu. Inu mumapeza maapulo kuchokera mu mitengo ya maapulo. Inu mumapeza minga kuchokera mu mitengo ya minga. Ndiko kulondola.

Tsopano, mvetserani mwatcheru kwenikweni tsopano.

Atatikonzeratu ife ku kukhazikidwa kwa ana mwa Yesu Khristu kwa iyeyekha, molingana ndi zake, mwa kufuna kwake kwabwino kwa chake—chifuniro chake,

Atatikonzeratu ife, kwa matamando a ulemerero wake wa chisomo chake, momwe iye watipanga ife olandiridwa mwa wokonedwa.

¹⁵⁹ Ndani anachita izo? “Chifukwa ine ndinasiya kumwa? Chifukwa ine ndinasiya kusuta?” Ayi. Iye anachita izo. Iye anandipanga ine, asanaikidwe maziko a dziko, wokhoza kulandiridwa mu kukhalapo kwa chisomo Chake. Palibe chimene ine ndinachichita. Sindinachite kanthu nkomwe pa izo. Ndinalibe kanthu kamodzi koti ndichite pa izo.

Ine ndinali nkhumba, pa kuyamba komwe. Ine ndinali wochimwa ndinabadwa mu banja la zidakhwa, ndinaleredwa kotchezera kachasu, nditakhala pa mbiya ya jang'ala, zochititsa manyazi. Ndiko kulondola. Mowa waku Kentucky, sindinkavala konse nsapato mpaka ine nditakhala mnyamata wamkulu. Tsitsi likulendewera pansi kumbuyo kwanga, nditakhala apo pa mtsuko wa kachasu, ndikutcheza kachasu.

Komabe, Mzimu Woyera unabwera kwa ine, pa usinkhu wa zaka seveni, anati, “Usati udzakhudze dontho la iwo. Ndipo usadzati udzapusitsidwe ndi tasungwana tating'ono ito kunja uko. Ndipo usadzati udzasute ndudu kapena kutafuna fodya wotafuna.” O, mai! Chinali chiani icho? Chifuniro chabwino cha Atate, asanaikidwe maziko a dziko, kuti Iye akanadzanditumiza ine kuti ndizilalikira Uthenga ndi kumatsogolera nkhusa Zake. Mulungu amudalitse Iye ndi, kwanthawizonse, Dzina lalikulu ilo! Ine ndizikhala pafupi ndi Baibulo Lake, kumira kapena kugwera mmadzi, wotchuka kapena wosatchuka. Kaya aliyense azindikonda ine, kapena ayi, ine ndizinkondweretsa Iye. Ine ndikufuna kuti ndizichita chimene chimamukondweretsa Iye.

¹⁶⁰ Ngati Abaptisti andikana ine, Amethodisti; Apentekoste, pa “umboni wawo woyambirira, kuyankhula mu malirime, kuti ndi Mzimu Woyera.” Ndicho chifukwa ife si Achipentekoste. Ife sitimakhulupirira kuti kuyankhula ndi malirime zimakupanga iwe kudzazidwa ndi Mzimu Woyera, monganso ife sitimakhulupirira kuti kukhala mu barani kungakupange iwe nkhumba. Ayi, bwana. Monganso ife sitimakhulupirira pokhala mu—mu nyumba yachifumu kuti zingakupange iwe mfumu. Sichoncho! Iwe ukhoza kukhala uli wantchito. Mwaona? Iwe ukhoza kukhala uli chirichonse. Ayi, bwana.

¹⁶¹ Ife timakhulupirira kuti iwe umalandira Mzimu Woyera mwa chokuchitikira, osati mwa lingaliro laluntha lopeka la Malemba, koma mwa chokuchitikira chomwe iwe wekha umachidziwa. Tsopano, ngati inu mukufuna kuti mudziwe ngati unali Mzimu Woyera, mupenye momwe moyo wanu ukugwirizanira ndi izo. Izo zikuuzani mtundu wa mzimu umene unabwera mwa inu.

¹⁶² Inu mukhoza kuyankhula ndi malirime ndipo mukhoza kusatero. Koma chifukwa chiani Achipentekoste amachita chinthu choipa monga icho? Mvetserani izi. Nchifukwa chiani Achipentekoste amachita izo. Bwanji? Chifukwa, pa chiyambi, pamene Mulungu anayamba kubwezeretsa kutali uko, zaka forte zapitazo, akubweretsanso mphatso, winawake anayamba kuyankhula ndi malirime. Ndipo kuyankhula mmalirime ndi mphatso yotsiriza, malingana ndi kuphunzitsa kwa Paulo, mwa mulu wonse wa mphatso. “Yaing'ono kwambiri ya mphatso zonse, ndi kuyankhula mmalirime.” Ndipo mwamsanga pamene iwo anachita izo, iwo onse anatengeka nazo ndipo anapanga

chipembedzo, ndipo anachitcha icho General Council, chomwe chiri Assemblies of God.

¹⁶³ Tsopano, ine ndayankhulapo kwa ena a amuna awo opambana, azamulungu awo opambana, ndipo iwo amati, “M’bale Branham, inu mukulondola. Koma ife tingachite chiani tsopano? Ngati ife tingauke motsutsa izo, ife tingatulutsidwemo. Ndipo kodi mpingo wathu udzaganiza chiani za ife? Pamene, ife tawaphunzitsa iwo kwa zaka, ife tawaphunzitsa iwo kwa zaka, kuti, ‘Umboni wa Mzimu Woyera ndi kuyankhula mmalirime.’ Bwanji ngati ife titasinthe izo tsopano?” Ndilo themberero la chipembedzo.

Ambuye adalitsidwe! Ife tiribe chipembedzo. Basi momwe Mzimu ukutsogolera, ife timatenga Izo.

Ubatizo wa Mzimu Woyera ndi chokuchitikira pawekha.

¹⁶⁴ Ine ndawonapo anthu akuyankhula ndi malirime. Ine ndaziwonapo mfiti zazimuna ndi zazikazi. Mmishonare aliyense akudziwa mofanana, yemwe anayamba wachitapo ndi aufiti ndi ziwanda. Ine ndaziwonapo izo zikuima ndi kuyankhula mu malirime, ndi kuponyera dothi paseri pa mitu yawo, ndi kudzidula okha ndi lezara, ndi kumayankhula ndi malirime ndi kuzitanthauzira izo. Ndipo inu mukuti umenewo ndiwo Mzimu Woyera? Ndithudi, iwo suli. Ndi chiwanda.

Yesu sananene konse, “Ndi malirime awo inu mudzawadziwa iwo,” koma, “Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo.” Ndipo Aefeso 5:1 amanena, kuti, “Chipatso cha Mzimu ndi chikondi, chimwemwe, mtendere, kupirira motalika, ubwino, kudekha, chipiriro, kufatsa, chikhulupiriro, kudziletsa.” Ndi kulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndi inu apo.

¹⁶⁵ Tsopano, ngati muli wa Methodisti, zipatso za mtundu umenewo zimakutsatirani inu, kuti sindinu wopsya mtima msanga, momenyana ndi macheke; ngati inu muli nako kupirira, pakuti inu muli nacho chikondi, ndipo ndinu woganizira aliyense; ngati chikondi chanu choyamba chiri Khristu, chachiwiri chanu chiri kwa munthu mzanu, inu kulola kukhala wachitatu, kumatsika monga choncho; ngati inu mukusunthira patsogolo, muli nako kupirira-kotalika, kufatsa, kupirira, chikhulupiriro. “Mai,” inu mukuti, “Mzimu wa Ambuye uli pa ine. Ndipo pali machiritso Auzimu. Mzimu Woyera uli chimodzimodzi lero.”

¹⁶⁶ Tsopano, inu mukuti, “Dikirani miniti. Ine ndimaphunzitsidwa mu mpingo wa Khristu. Masiku a zozizwitsa anapita.” Iwe uli ndi chiwanda. Ndiko kulondola.

Inu mukuti, “Chabwino, ife tiyenera kuti tizibatizidwa. Mu Baibulo, mulibe chinthu choterocho ngati kubatizidwa mu dzina la ‘Atate, Mwana, Mzimu Woyera.’ Ine ndikuziwona izo pakali pano. Izo ziri mu Lemba. Ndi Dzina la Ambuye Yesu. Paliponse, ndi Dzina la Ambuye Yesu.”

Oyera a Kuwala nenani,
 Yesu, kuwala kwa dziko;
 Mabelu Akumwamba alira,
 Yesu, Kuwala kwa dziko.

Aliyense, mu maonekedwe akupembedza tsopano.

Tiyenda m'kuwala, kukong- . . . (Ingoigwirani
 iyo miniti, mwaona.)
 Kumabwera komwe mame achifundo ali;
 Kuwala ponse, usana ndi usiku,
 Yesu, Kuwala kwa dziko.

¹⁷² Kodi inu simukanafuna kukhala naye Yesu ndi Mawu Ake, kusiyana ndi kukhala nalo lingaliro lirilonse la chipembedzo pa izo? Ndi angati akanati bola akhale naye Yesu ndi Mawu Ake? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

Tsopano, pezani malo amodzi umu pamene Mulungu anadzoza konse chipembedzo. Apezeni malo amodzi pomwe Iye anamuikapo konse mlaliki wachikazi kapena anadzozapo mmodzi, mu Malemba. Apezeni malo amodzi pamene munthu aliyense anayamba wakonkhedwapo kapena kutsanuliridwa. Apezeni malo amodzi pamene aliyense anayamba wabatizidwapo mu Dzina la Yesu Khristu, paliponse, pomwe pali lirilonse kupatula Dzina la Yesu Khristu; osati “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.” Mupeze pamene munthu mmodzi anayamba wabatizidwapo mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.” Mubwere mudzandisonyeze ine. Paliponse, munthu anabatizidwa mu Dzina la Yesu.

¹⁷³ Tsopano ife tikupitirira mu zinthu zakuyapo kuposa izi tsopano. Tsopano ife tikulowa mu “umboni woyambirira,” ndi zina zotero, ndi kungoti tiwone pamene izo ziri.

Tsopano, ngati iwo amaphunzitsa mosiyana ndi izo, iwo akuphunzitsa zinthu zomwe mulibe mu Baibulo.

¹⁷⁴ Kumbukirani, ine ndikukufunsani inu malo amodzi pomwe anayamba akhala ndi chipembedzo. Mungondisonyeza ine amodzi. Ndiye winawake akulakwitsatu. Ine sindikufunsa kuti akhalepo amodzi *apa* ndi ena cha *apo*, mwinamwake, ngati enawo panalibe. Ine ndikukusonyezani inu. Mundisonyeze ine malo amodzi pamene panayamba pakhala chipembedzo, zaka firii handiredi atamwalira mtumwi wotsiriza. Mundisonyeze ine pamene pali chipembedzo chimodzi kunja kwa mpingo wa Katolika kuyambitsa izo. Mundisonyeze ine malo amodzi pamene Baibulo silimatsutsa zipembedzo. Ndiye nchifukwa chiani inu muli chipembedzo?

¹⁷⁵ Mundisonyeze ine malo amodzi, tsopano, malo amodzi, malo amodzi pamene munthu aliyense anakonkhedwa konse, kwa kukhululukiridwa kwa machimo awo. Ine sindikutanthauza amodzi okha *apa* ndi *apo*. Tsopano ndisonyezeni ine malo amodzi mu Lemba lonse. Mundisonyeze ine malo amodzi mu

Lemba lonse pamene wina anayamba watsanuliridwa, kwa kukhululukiridwa kwa tchimo lawo. Mundisonyeze ine malo amodzi pamene aliyense anayamba wabatizidwa konse mu dzina la Ye- . . . Atate, Mwana, Mzimu Woyera. Malo amodzi okha, munthu mmodzi, pamene munthu mmodzi anayamba wabatizidwapo mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.”

Mundisonyeze ine malo amodzi pamene Mulungu anayamba waika konse mlaliki wamkazi mu mpingo, kapena mwina ananena kuti adzakhalapo. Ziri pati izo?

Icho ndi chitsutso chachikulu. Koma ine ndikufuna ndilipeze funso lanu, tsopano, liri pa guwa, likundisonyeza ine pamene china cha zinthu izi chiri; usikuuno, ine ndidzapepesa. Ngati izo palibepo, ndiye ngati inu simunakwaniritse zofunikira izi, nanga bwanji osazikwaniritsa izo? Bwerani mudzakhale mmodzi wa ife. Inu muli, chonchobe, mwakungoyankhula.

¹⁷⁶ Ngati dzina lanu liri pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, inu muziyenda mu Kuwala, inu mukuwona Kuwala. Mulungu akuulula Izo, ndipo inu muziyenda mu Iko. Ndiko kulondola ndendende. Mwaona?

¹⁷⁷ Tsopano chiani? Ine sindiri kukutengerani inu mobwerera ku mpingo. Ine ndikukutengerani inu mobwerera ku Baibulo. Tsopano, kodi Paulo anati chiani? Kodi Paulo anati chiani? “Ngati mngelo wochokera Kumwamba alalikira china chirichonse chosiyana ndi *Ichi*, msiyeni iye akhale wotembereredwa.”

¹⁷⁸ Mulungu anati, “Mulole mawu a munthu aliyense akhale abodza, ndipo Anga akhale Choonadi.” Chotero ine sindikusamala chimene mpingo uliwonse unena, Achipentekoste, Abaptisti, Apresabateria. Mawu a Mulungu ndiwo Choonadi. Nchifukwa chiani iwo anayambitsa izi? Pa kuwerengera zipembedzo.

¹⁷⁹ Assemblies of God Achipentekoste, lero, angapereke chirichonse, mpaka pansu pa mitima ya aziphunzitsi aakulu awo, ngati iwo akanati asayambe konse mbalume iyo ya “umboni woyambirira: kuyankhula mu malirime.” Iwo akudziwa kuti nkulakwitsa. Izo zizingasunge madzi. Ndithudi zizingatero. Ine ndikhoza kutsimikizira kwa inu ndi Baibulo la Mulungu kuti inu simumalandira Mzimu Woyera pa kuyankhula ndi malirime. Izo siziri mkati Umu. O, inu mukuganiza; eya, zedi. Izo zinalembedwa mwa pafupi kwambiri mpaka izo zikanawanyenga Osankhidwa omwe. Mwaona?

“Iye anazibisa izo kwa maso a anzeru ndi aluntha, ndipo amaziulula izo kwa makanda.” Ilo ndi vumbulutso lauzimu. Inu muliwone vumbulutso likugunda izo, ndipo muwone izo zikuwalira apo. Onani, ndi inu apo. Mwaona? Icho ndi chinthu chimene inu mukufuna kuti muzichisamala, abwenzi, onani, ndi pamenepo.

¹⁸⁰ Ife tikumuthokoza Mulungu chifukwa cha Mzimu Woyera Yemwe ali Mphunzitsi wathu. Ndipo iye samangopita kunja ndi kukatenga kalingaliro kena kopeka, ndi kukabweretsa iko kuno nkuti “O, aleluya! Ndi izi pano, zolondola, zinalembedwa apa pomwe. Aleluya!” Mzimu Woyera umapita mmbuyo ndi kukubweretsani inu mpaka kupyola mu Lemba lonse, nkumukha zikitsa iye apo pomwe, kudutsa kumene mu lemba. Mwaona? Ndi pamene inu muli nacho Choonadi. Ndizo ndendende. “Pakuti langizo liyenera kukhala pa langizo pa langizo, ndi mzere pa mzere pa mzere.” Ndi momwe Baibulo linanenera kuti tizichitira izo.

¹⁸¹ Inu mukuti, “Kodi inu mukunyoza chipembedzo?” Ayi, bwana. “Kodi inu mukunyoza akazi olalikira?” Ayi, bwana. “Kodi inu mukunyoza kuyankhula mu lirime?” Ayi, bwana. “Kodi inu mukuwanyoza anthu awa omwe anabatizidwa mu dzina la ‘Atate, Mwana, Mzimu Woyera?’” Ayi, bwana. Ayi, bwana. Koma, ine ndikuti, ngati iwo akudziwa bwinoko tsopano, Mulungu adzawaimba iwo mulandu ngati iwo sakutsatira mu Kuwalako. Inu mukhoza kukhala musakudziwa izo mpaka pano, koma inu mukuzidziwa izo kuchokera pano. Mwaona?

Tsopano, ngati inu simukuganiza kuti uko ndi kulondola, fufuzani Malemba. Ndiye mupeze malo anu, ndipo mubwerere ndipo mudzaziye izo pa tebulo ili usikuuno, ndipo ife tiwona ngati ziri zolondola kapena ayi. Ndiye inu mupite mukafufuze Izo, ndi lingaliro lotseguka, mtima wotseguka.

¹⁸² Tsopano, izo, tsopano, kuphunzitsa uku monga chonchi ndi kwa Branham Tabernacle, mwaona, kuno kokha, komwe kuno basi. Kulibe . . .

¹⁸³ Ine ndikukhumba akanati asakhale ali “Branham Tabernacle.” Ine ndikukhumba iye akanangomatchedwa “Kachisi,” akanati akhale wopanda ngakhale dzina langa litaikidwa pa iye.

¹⁸⁴ Ine ndikukonzekera kuti ndichisithe tchalitchi chino . . . Inu nonse mukudziwa, pamene ife tinkagula icho, ine ndinagula apa pamene ine ndinkagwira ntchito ku Kampene ya Public Service. Ndipo ndinaika chinthu ichi cha kuno, ndipo ndinangochitcha icho limenelo chifukwa kuti M’bale Seward ndi iwo anaika dzina langa kwa icho pamene iwo ankaliyika ilo pa chikalata kumusi uko. Mwamsanga basi pamene ine nditi ndithane nacho chinthu ichi chimene ife tirimo tsopano, mpingo uno udzaperekedwa kwa akuno awa, ndipo basi chingoperekedwa; dzina langa lichotsedwapo pa icho.

¹⁸⁵ Ine sindikuganiza dzina langa liyenera kukhala pa tchalitchi chimenecho. Icho sichikuyenera kukhala chiri “Branham Tabernacle.” Icho chikungoyenera kukhala tchalitchi, “Mpingo wa Ambuye Yesu Khristu,” kapena chinachake monga choncho. “Kachisi wa Ambuye,” onani, “Malo okhalamo,” “Nyumba ya

pemphero,” kapena chinachake, chimzake, kuchipatsa dzina la mtundu wina. Muwalole osonkhana asankhe dzina lawo. Dzina langa, langa—ndine munthu chabe. Dzina langa silikuyenera kukhala pa ichi, mosaposa kanthu kena. Chinthu chomwe anaikira dzina langa pa ichi, chifukwa dzina langa linali pa chikalata, anati, “Billy Branham.” Mwaona? Ndipo ilo silikuyenera kukhala choncho. Ayi, bwana. Iwo uyenera kukhala mpingo wa akuno. Ichi, ichi chiyenera kukhala cha—osonkhana panowa.

¹⁸⁶ Ndipo mpingo uwu ndi woima pawokha. Palibe gulu la matrasti kapena madikoni angakuuzeni inu zoti muzichita. Mpingo uno, mu voti yonse, zimakuuzani inu zoti muzichita. Ndizo ndendende kulondola, ngati pali lingaliro.

¹⁸⁷ Ngati inu simukumukonda m’busa wanu, ndipo pali anthu awiri kapena atatu ali ndi chinachake chomutsutsa m’busa, iwo sangakhoze kuima ndi madikoni awo, matrasti, iwo angokhala pa udindo omwe ali nawo pano. Iwo ali nayo voti imodzi yokha. Ndizo zonse. Ngati iye ali m’busa wothandizira, iye ali nayo voti imodzi yokha. Iye ali ngati monga membala wamba yemwe ali kumbuyo uko. Voti yonse ya mpingo imathetsa vutolo. Ndipo uko nkulondola. Ndi—ndi kulondola. Palibe gulu la madikoni limene lingamuchotse m’busa, kapena palibe m’busa yemwe angalichotse gulu la madikoni. Mpingo umachita zimenezo, mu voti ya aliyense pa chinthu chonsecho.

¹⁸⁸ Iwo ndi woyima pawokha mwa wokha. Ife tiribe mabishopu. Ife tiribe oyang’anira konsekonse. Ife tiri naye Yesu. Ameni! Iye ndiye Bishopu. Iye ndiye Woyang’anira Konsekonse. Iye ndiye M’busa Wamkulu. Iye ndiye Mfumu. Iye ndiye Ambuye. Iye ndiye Mchiritsi. Iye, ali Zonse—mu—Zonse. Ndipo ndife omumvera Ake basi, tikuyenda mu Kuwala. Ameni.

¹⁸⁹ “Ndipo Iye anawaika ena mu Mpingo.” Chiani? “Mu Mpingo,” mu Thupi. “Anawaika ena mmenemo.” Chiani?

“Poyamba atumwi,” ndiwo amishonare. Ife tiri naye wina mu tchalitchi muno tsopano, mnyamata wamng’ono kumbuyo uko, mzanga kwa ine, m’bale, ine ndimamutchi iye Creech Jefferies. Ndiko kuitana koyamba, kwapamwamba, umishonare. Inu mukuti, “Mtumwi ndi mishonare?” Mwamtheradi. Pitani mukayang’ane mu dikishonare ndipo mukapeze chomwe *mtumwi* amatanthauza; amatanthauza, “wina wotumidwa.” Pitani mukayang’ane, ndi chomwe *mishonare* amatanthauza, “wina wotumidwa.” Chinthu chomwecho. Dongosolo lapamwamba kwambiri ndi mmishonare yemwe amayenda pa nyanja chifukwa cha Ambuye Yesu. Pamwamba, “Poyamba atumwi.”

¹⁹⁰ “Achiwiri, aneneri.” Kodi mneneri ndi chiani? Mpenyi. Osati wina yemwe amangodzipanga . . .

Osati mtumwi yemwe amangodzipanga ngati kuti iye ndi mmishonare ndi kumakhala kwao, koma uyo yemwe ali mmishonare weniweni.

Ndipo mneneri, mpenyi.

¹⁹¹ Atumwi, aneneri, aphunzitsi, alaliki, abusa, ndi zomwe Thupilo liri nazo.

Mu thupi wamba ilo, ndiye, muli mphatso zauzimu naini. Imodzi ya izo ndi nzeru, chidziwitso, machiritso Auzimu, kuyankhula mu malirime, kutanthauzira kwa malirime, mphatso zonse zosiyana izi zomwe ziri mu thupi wamba.

Ndipo atumwi awa, abusa, aphunzitsi, ndi alaliki, onse ali pano kuti azitsimikizira kuti, mu mphatso izi, zinthu izi zikugwira ntchito bwino. [M'bale Branham akukhwatchitsa chala chake kamodzi—Mkonzi.] Ngati iwo apeza chinachake chabodza chikuukapo, mwamsanga iwo amachitsutsa icho, chifukwa icho sichiri molingana ndi Lemba.

Mumulole wina abwere apo, nkuti, “Mulungu adalitsidwe, ine ndiri ndi mafuta mmanja mwanga. Penyani *kuno*. Inu mukudziwa, ine—ine—ine ndikukhulupirira ndiri nawo Mzimu Woyera, ndipo ndiri nawo mafuta mmanja mwanga.”

¹⁹² Inu mumamumva wina akuti, “Izo siziri Mwamalemba.” Ndiko kulondola. “Tiyeni tizitenge izo ndipo tipite mu chipinda umo. Tiyeni tifufuze Malemba bwino bwino. Mundisonyeze ine mu Malemba pamene izo ziri, umboni wa Mzimu Woyera.”

¹⁹³ Wina anati, “O, ine ndinayankhula ndi malirime. Ine ndiri nawo Iwo.”

“Ndisonyezeni ine mu Malemba uwo uli umboni wa Mzimu Woyera.” Ndiko kulondola.

¹⁹⁴ “O, Ambuye anandiitana ine kuti ndizilalikira,” akutero mkazi wina.

“Ndisonyeze ine mu Malemba iye akuchita izo.” Eya.

¹⁹⁵ “O, ine ndikudziwa Ambuye andiuzwa ine. Iye anandidalitsa ine usiku uja pamene ine ndinabatizidwa mu dzina la ‘Atate, Mwana, Mzimu Woyera.’”

“Mundisonyeze ine mu Malemba pamene inu mukuyenera kuti muzichita izo.”

¹⁹⁶ “Chabwino, ine ndiri basi monga wina aliyense, ndipo ndine wa Methodisti, kapena wa Baptisti, kapena wa Presbateria. Ndine wa Chipentekoste.”

“Ndisonyezeni ine mu Lemba pamene Mulungu ananena zimenezo.” Mwaona? Ndiko kulondola. Izo siziri umo.

¹⁹⁷ Tsopano, apa pali kutsutsa kotseguka-kwambiri kwa inu mamembala a kachisi uyu. Pali kutsutsa kotseguka kwambiri. Tsopano, ngati inu muti mupeze chinthu chimodzi chimene inu mukuganiza kuti chiri cholakwika, chimene ine ndachinena

mmawa uno, chinthu chimodzi chomwe chiri chotsutsana ndi Lemba, ndinu okakamizidwa kuti muchiyike icho pa guwa ili usiku uno. Ndiko kulondola. Inu muchibweretse icho ndipo mudzachiyike icho pano. Mundisonyeze ine Lemba, ndime mu Baibulo pamene akuti panali chipembedzo, kuti Yesu anapanga chipembedzo, kapena chirichonse cha zinthu izi zimene ine ndaphunzitsa. Penapake pamene Iye anayamba wadzoza ndi kumuika mkazi mu mpingo, ngati mlaliki; penapake Iye anayamba waloleza kukonkha, kutsanulira; kapena—kapena chirichonse cha mtundu umenewo chimene ine ndinali ndikuyankhulapo. Muchiyike icho apa.

Ndiye, usikuuno, ife tikupita umo, ngati Ambuye alola, ku “ubatizo wa Mzimu Woyera,” ndi mu “mbewu ya serpenti, ndi ya mkazi.” Chabwino. Ambuye akudalitseni inu. Ndi angati akumverera bwino?

O, ndifuna ndipiteko,
O, ndifuna ndipiteko;

Tsopano iyimbeni iyo mokoma kwenikweni kwa Ambuye.

Kwathu Kumwamba kowala bwino,
Ndifuna ndipiteko.

O, ndifuna ndipite, ndipiteko,
O, ndifuna ndipite, ndipiteko;
Kwathu Kumwamba kowala bwino,
Ndifuna ndipiteko.

[Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

¹⁹⁸ Tsopano, pakhala pali chinthu chimodzi chikhalireni ine ndiri pa izi nthawi yonseyi kwa masabata angapo awa, ine ndinapeza, lomwe liri vuto ndi ine. Ndipo ine ndikufuna kuti ndivomereze izo tsopano kwa mpingo wanga. Ine ndinakhala kuseri kwa mitengo ya mithundu ndi migwalangwa iyo, kumusi kuno ndikufufuza, “Kodi ndi pati pamene ine ndinapanga kulakwitsa kwanga koyamba? Nchiani chinandipanga ine kupita molakwika? Chinali chiani icho?” Inu mukudziwa chimene ine ndinachipeza chimene chikundipanga ine kulakwitsa? Pali chinthu china monga kupita mowirikiza ndi chinachake. Kodi inu mumadziwa izo? Iwe ukhoza kuyesera kuti uzikhala wolondola bwino, ndi kuyesera kukhala wabwino, ndiyeno iwe ukhoza kukhala wabwino mopitirira. Ndipo ine ndimangowalola anthu kumandikakhira ine uku ndi uko. Mwaona?

Iwo amati, “Chabwino, M’bale Branham, inu mubwere kuno. Ambuye anandiuza ine kuti ndikuuzeni inu izi.”

“Chabwino, ziri bwino, m’bale, ine ndibwera.”

“O, M’bale Branham, inu musati mupite *uko*, cha *kuno*.”

199 “Chabwino, mwina ine kulibwino ndisati ndipite uko.” Mwaona? Ndipo iwe sukudziwa choti uzichita. Ndi chimene chimandipanga ine kukhala wamanjenje.

Ine ndizipita kumene Ambuye azinditsogolera ine kuti ndizipita, ndipo ine sindikusamala zomwe aliyense azinena pa izo. Mwaona? Ndizo ndendende kulondola. Chotero, ine sindipweteketsa kumverera.

200 Ndiyeno ine ndinazindikira chinthu chinanso. Ana anga kuntunda uko asanduka gulu la amanjenje, kumakuwa usiku, ndi chirichonse, anthu akumawunjikana mkati ndi kunja kwa nyumba iyo, nthawizonse, anthu kumabwera kuchokera kulikonse. Ine sindikuti akulakwa anthuwo pa izo, anthu odwala. Koma ife tazikonza izo zonse.

Ndipo kuno ku tchalitchi, pamene ine ndibwera kudzachititsa msonkhano, bwanji, ine ndimatsala pang’ono kuti ndizembe, kutuluka mu tchalitchi, chifukwa anthu amangokugwirabe, ndi *izi* ndi *izo*. Ndiri wotopa kwambiri, ndipo nthawizina potuluka ku msonkhano wa machiritso, ndipo ndisali bwino kwenikweni kwa iwo, ine nkuti . . .

“Timati, M’bale Branham, Ambuye anati . . .”

“Eya. Pamene ife tinabwera kuno, kupita . . .” Izo si zabwino ayi. Ine ndisamachite izo. Ife sitimasowa kumachita izo.

201 Tsopano ife takonza ndondomeko yoti izisamalirira izo. Ndipo tsopano, ingokumbukirani, aliyense yemwe akufuna . . . ine ndikufuna kumamuwona aliyense. Ndipo ine ndikufuna kumakhala nayo nthawi, ndi kumayankhula nawo anthu. Mwanjira iyi, iwe sungakhoze. Iwe umapeza munthu wina mmenemo, ndipo, chinthu choyamba inu mukudziwa, nthawi yako yonse yapita kwa mmodzi, ndi—ndipo iwe sumafika poti umuwone winayo. Ndipo izo si zabwino. Anthu amabwera kuchokera ulendo wautali, kuti adzangokhala ndi mawu pang’ono nawe. Ndipo ngati Mulungu wa—wawapatsa anthu amenewo chikhulupiriro icho mwa ine, kuti akukhulupirira izo, iwo akuyenera nthawi ya pang’ono yoti aphunzitsidwe. Iwe sumayenera kungowabweza iwo, nkuti, “Ayi, ine sindiwonana ndi aliyense.” Izo si zabwino. Chifukwa, ine ndikuchita mantha kuti ndichite izo, chifukwa . . .

Wina amabwera nkuti, “Tsopano, Ambuye akundiiza ine, M’bale Branham, kuti inu muzichita chinthu *chakuti*, *chakuti*. Ichi ndi—ichi ndi chifuniro cha Ambuye tsopano.” Ambuye andiiza ine chifuniro Chake.

202 Bambo King, ndi angati akumukumbukira R.A. King, anakonda kubwera kuno, ali cha kuno? Iye anati . . . Ine ndinali kumanga ngalawa uko, nthawi yina. Iye anati, “Tsopano, M’bale Branham, inu muzimanga ngalawa iyo molingana ndi kulingalira kwanu kwanu.”

203 Anati, “Ine ndinali kumanga...Kapena, munthu wina ankamanga ngalawa nthawi yina, ndipo mnyamata anadza apo, anati. ‘Inu mumayenera kuti mudule mmphepete umu mwa njira *iyi*.’ Chabwino, iye anayesera izo mwa njira imeneyo. Winanso anati, ‘O, inu mukuyenera kuti muchite izo mwanjira *iyi*, chirichonse, m—mnthiti ndi chirichonse. Ngalawayi ikuyenera kuti ikhale mwanjira *iyi*, ndipo ipindike mwanjira *iyi*, ndi mutu, ndi mmbuyo, n—ndi makwerero.’”

204 Ndipo iye anati, “Icho chinali chinthu chowoneka moyipa chimene inu munayamba mwachiwonapo, pamene iye anatsiriza.” Anati, “Iye anangotenga ngalawayo ndi kukaisiya iyo kuseri. Ndipo anayamba ndi macheka ake, kudzichekera inanso.”

205 Anati, “Winawake anabwerapo nkuti, ‘Ndikuti, *umu* ndi momwe inu mukuyenera kumangira iyo.’ Anati, ‘Iyo apo, inamangidwa ndi malangizo a ena, ili kuseri uko. Ine ndikumanga iyi molingana ndi momwe ine ndikuganiza iyo ikuyenera kuti imangidwe.’” Ndiko kulondola.

206 Tsopano, Mulungu, ngati Iye akufuna kuti ine ndichite chirichonse, Iye andiuzwa ine choti ndichite. Ngati inu mukuganiza kuti ine ndikulakwitsa mu zomwe ine ndikuchita, kapena chirichonse chonga izo, inu mundipempherere ine, kuti Mulungu andiwongole ine. Mwaona? Chifukwa ine sindingakhoze kumamvetsera kwa ochuluka mopitirira.

207 Tsopano, inu pano mwinamwake pa mpingo, iwe umangoyenera kuti uzimvera kwa mwinamwake mmodzi kapena anthu awiri, koma kuno ine ndimapita mu makumi a zikwi. Ine ndingamachite motani izo? Ndiye ine ndinati, “Ine ndisanamupange munthu wina kukhala yankho, ine ndizikhala pansi ndi kuziwerenga izo mobwereza bwino, kuwona njira yomwe Mzimu Woyera uti unditsogolere. Ndiye ine ndizikamuza iye kapena mkaziyo, chirichonse chomwe chiri, ndipo ilo ndi lingaliro langa. Ine ndizikakamira pa ilo. Ndiko kulondola, kukhala apo pomwe.”

208 Tsopano, zoyankhulana zakonzedwa. Aliyense yemwe akufuna kuti andiwone ine, zabwino mwangwiro, ngati inu mungambire ku BUTler 2-1519. Muzingoyang’ana mu bukhu la mafoni ndipo muzipeza William Branham, BUTler 2-1519, dongosolo lizikonzedwa la kuyankhulana. Izo zizilebedwa, ndendende basi nthawi ndi malo okachitira izo. Ndipo ine ndikhoza kukomana ndi munthu aliyense, kuwonana nawo, kuwathandiza iwo pa mavuto awo ndi zinthu. Koma ine sindingati ndizingolowa umo nkukhala tsiku ndi mmodzi, ndi maora foro kapena faifi ndi mmodzi *uyu*, ndipo tsiku lotsatira ndi kuphonya chinthu chonsecho. Ife tiri nayo nthawi yochulukuka *motero* basi. Ife tiziwafunsa iwo zomwe akufuna, ndi kuchulukuka kwa nthawi, ndi kuzibweretsa izo apo pomwe. Ndipo ife tizimuwona munthu aliyense. Ife tiri nazo izo.

209 Ndipo bambo yemwe aziyankha mafoni akhala ali Bambo Mercier kuno, kapena Bambo Goad, akhala apo pomwe. Ndipo iwo azizikonza izo bwino bwino mu bukhu langa, ndendende, za kuyankhulana, ndipo ine ndizimuwona munthu aliyense.

210 Ngati ilo liri vuto lapadera, ngati ili nthawi ya msonkhano wa pemphero tsopano, wa odwala, muziwabweretsa odwala anu ndi osautsika mkati ndi kuwalola iwo amvetsere usiku kapena uwiri, tsopano. Ife tizipempherera zofunikira mwamsanga izo.

211 Komano, pambuyo pa pafupi mausiku angapo, ine ndikufuna kuti ndikuyamba pa utumiki wanga watsopano, ndipo ine ndikufuna ndiziwatengera iwo mmbuyo muno mu chipinda chino. Chifukwa, inu mukuwadziwa masomphenyawo. Ndi angati akuwakumbukira masomphenyawo? Zedi, inu muli. A hema wamng'ono mu chipinda.

212 Tsopano, ine ndizimutenga Meda umo limodzi nane, pa usiku woyamba, pa chifukwa cha kutumiza akazi mmenemo. Ndiyeno ngati izo. . . Tiwone momwe izo zikugwirira ntchito ndiri ndi iye mmenemo. Ndiyeno ngati izo sizimagwira bwino ntchito, mwanjira imeneyo, ndiye ine ndisintho ndi kumatumizamo akazi awiri pa nthawi, kuwabweretsa akazi awiri pa nthawi imodzi, chifukwa iwo akubwera mu malo omwe muli mwamuna yekha. Mwaona? Ndipo izo, ndithudi, ife tiri ndi malingaliro oyer. Koma Mdierekezi alibe awo kunja uko, inu mukuona, chotero zomwe iye angaganize pa izo, mwaona, ndi zomwe dziko liti linene.

Koma ndi utumiki umene ine sindingakhoze kuulola kuti udziwike kwa gulu. Palibe mmodzi yemwe adzachitepo moonera izi. Inu mukuona? Ayi, bwana. Ayi. Ine ndikudziwa kuti izo ziri potulukira pomwe tsopano. Ine ndikukhoza kuwona ngati ndikhoza kungofikira apo ndi kuchigwira icho. Izo ziri pomwepa.

213 Usiku watha ine ndinali kulota basi ndisanauke mmawa uno, M'bale Neville. I—ine ndinali kulota loto. Ndipo ine ndimaganiza utumiki. . . Ine sindikudziwa chimene ndinali kuchita. Koma, chirichonse chomwe icho chinali, o, inu mukanena za zinthu zikuchitika, ine sindinayambe ndaziwonapo zoterozo. Ine ndinawuka ndikungolira, kumamutamanda. Ine ndinamumenya mkazi wanga mu nkhope ndi dzanja langa, monga *choncho*—monga *choncho*, kumangomutamanda Mulungu, nditagona apo.

O, i—ine ndikungodziwa kuti pali chinachake komwe kuno chomwe chakonzekera kuti chifikire ndi kuchigwira icho. Ichu chikhala chiri chachikulu kuposa zomwe zakhala ziri. Ichu chikhala chodabwitsa. Ine ndikukhulupirira Mulungu akukonzekera kuti achite chinachake chachikulu. Koma tsopano ife tiyenera kuchifikira icho mwabwino bwino, mwaluntha, ndi mwa Mawu a Mulungu momwe. Kulondola. O, ife timamukonda Iye.

²¹⁴ Tsopano kumbukirani, ngati aliyense wa abwenzi anu kapena aliyense yemwe akufuna kuti andiwone ine ndipo akufuna kuti ayankhule kwa ine zokhudza chinachake chaching'ono chomwe chiri cha mwapadera, muwalole iwo andiyimbire BUTler 2-1519 ndipo padzakhala kukonzedwa kwa zokambirana ku maloko. Ine sindingakhoze kukhala nawo iwo ku nyumba yanga uko, ndi cha ku kachisi kuno, chifukwa inu mukabwera muno . . .

Ine ndimalalikira mochedwa kwenikweni. Ndipo ine ndimakhala kuno, chifukwa ine sindimakhala ndi inu mochuluka kwambiri. Ndipo ine ndimakugwirani inu motalika monga ine ndingathere, kuti nditengere Mawu aliwonse mmenemo. Chifukwa, abwenzi, iyi ndi nthawi yokha yomwe ife titi tichite konse izi. Izi zonse zitha, posachedwapa. Ife tikupitabe kumene ku chigwa, mpaka uko. Tayang'anani pa iwo omwe atsalira kuyambira chaka chathachi, omwe akhala ali kuno. Mwaona? Chotero ife tikupita mmusi mwa chigwa. Ife tiyenera kuti tizichite izi tsopano. Izi ziyenera kuti zichitidwe tsopano. Ndipo, tsopano, ndi chifukwa ine ndikukugwirani inu.

²¹⁵ Inu mukuti, “Chabwino, izo, nanga bwanji Lemba la izo?”

Eya, Paulo analalikira usiku wonse, usiku wina. Ndipo munthu anagwa mu nyumbayo, anadzipha yekha. Ndi angati akudziwa izo? Utali wa usiku wonse! Paulo anapita ndipo anakagoneka thupi lake pa iye, anamumverera iye, mtima wake unayamba kugunda limodzi ndi mtima wa mnyamata ameneyo, anati, “Ayī, iye . . .” [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

Titenge Dzina la Yesu nafe,
Kugwa modzilambatitsa pa mapazi Ake,
Mfumu ya mafumu Kumwamba tidzamuveka
Iye korona,
Pamene ulendo wathu udzatha.

Chabwino, mpaka ku mapazi athu.

Tenga Dzina la Yesu nawe,
Mwana . . .
. . . lidzakusangalatsa iwe.

Ine ndikukuuzani inu zoti tiyeni tichite. Tembenukani uko ndipo mugwirane manja ndi winawake apo, mukuti, “Inu muli bwanji, m'bale? Ine ndikutsimikiza ndakondwa kudziwana nanu.”



UBATIZO WA MZIMU WOYERA CHA58-0928M
(The Baptism Of The Holy Spirit)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu mmwa, Seputembala 28, 1958, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa m'chaka cha 2003 ndi Voice of God Recordings:

CHICHEWA

©2012 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org